

# **MUNABWERA KWA INE**

## **Buku Lophunzitsira Utumiki wa Kundende**

### **KUPEREKEDWA**

Bukuli likuperekedwa mwa chikondi kwa onse anairimbikitsa...

*Akazi aku malo a Central California Women*

Ndi kukumbukira amene ndinali naye pa ukapolo wokaphedwa

*Kara Faye Tucker*

*yemwe anachoka ku ukapolo wokaphedwa ndikupita mmanja mwa Yesu  
pa February 3, 1998*

### **Kuvomereza**

Bukuli lawunikiridwa kuchokera pa kaonedwe kosiyana siyana:

- M'busa wa kundede
- Mkaidi okanyongedwa
- Otumikira odziperekira otumikira mkwati mwa ndende.
- Odziperekira olingana ndi kukumana ndi akaidi m'modzi n'modzi.

Kuyamika kwapaderadera kupite kwa Catherine Thompson chifukwa cha kusintha zolembedza zoyamba za bukuli, mlongo wamtengo wapatali mwa Ambuye yemwe anali m'ndende ya akazi ndi akazi a CCWF



## ZAMKATIMU

## CHIYAMBI

Inu mwanyamula fungulo wa bokosi la chuma m'manja mwanu. Mkati mwa bokosi muli golide, siliva, ndi miyala yamtengo wapatali. Bokosi limene muli chumachi lodabwisa—losapasa chidwi. Lazungulidwa ndi waya wa lumo, mpanda wa magetsi, ndi nsanja yolondera ya zida. Koma mkati muli chumwa... abale ndi alongo, amtengo wapatala kwa Mulungu, omwe akukudikira INU.

Buku lomwe mwanyamula mmaja mwanu--“*Munabwera kwa Ine*”--ndi phunziro la utumiki wa ku ndende. Bukuli likupereka malangidzo a mulingu wina uli wonse omwe mungate gawo:

- Mlingo wochepa olingana ndi akaidi.
- Kukumana ndi akayidi m'modzi m'modzi.
- Ukumikira mu kulambira kwa pagulu, ma pologalamu apaderaera, kapena kusanthula Baibulo mkati mwa ndende.
- Kuthandidza mabanja a akaidi.
- Kupereka utumiki kwa akaiydi omwe atuluka ku ndende.

Ikuphatikidzanso malangizo a kavalidwe ndi malamulo zachitedzo, kufanidzitsa kwa ndende ndi akayidi, komanso m'mene mungakhalire ndi akaidi mu njira yomwe ingawapangitse kuti akhale ndi chidwi ndi uthenga wa Uthenga Wabwino ndi kulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wa moyo wawo.

Bukuli lapangidwa kuti likakhale phunziro lophunzitsira:

- Anthu omwe ali ndi kukhumba kofuna kutengapo mbali yautumiki wa kundende.
- Mipingo yomwe ikukonzekera kuyamaba utumiki wa kundende.
- Zipembedzo zomwe zikufuna kuti mipingo yawo izittengapo gawo pa utumiki wa kundende.
- Sukulu zophunzitsa Baibulo ziri ndi kukhumba kupereka utumiki wa kundende kwa ophunzira ake.
- Azibusa omwe akufuna chida chophunzitsira anthu odzipereka.

Chaputala china chirichonse chiri ndi zolina zopereka malangizo zotsogolera zokumana nazo pophunzira ndi mayeso oziyesa nokha pofuna kuyeza m'mene mukupitira patsogolo. (Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli ndipo atha kuchotsedwa ndi mphunzitsi ngati sakufuna kuti ophunzira awaone). Mu zakumapeto muli matanthauzo a mawu omwe amagwiritsidwa tchito ku ndende, malembo ogwirizana ndi ku ndende, ndi mndandanda wa zofunikira za utumiki.

Chaputala 13 cha bukuli ndi gawo la padera la ogwira ntchito mongothandidza, mpingo, mabungwe achikristu, kapena azibusa atha kuyikapo zipangidzo zophunzitsira zapaderadera za utumiki wa ku ndende-zinthu ngati mapu apamalopo, malamulo, mavalidwe, mafomu ndi zina zambiri. Ngati muli mphunzitsi yemwe mukugwiritsa ntchito bukulu ku sukulu la Baibulo, muntha kuyika zinthu zanu zomphunzitsira kapena zoonjezera mu Chaputala 13.

Muli ololedzera kuchulukitsa bukuli ku ulemerero wa Mulungu! Buku lonseli likupedzeka pa tsamba la intaneti pa: <http://www.harvestine.org>

## **Chuma mu maselo aku ndende**

### **Lolembedwa ndi Bill Yount**

Unali utsiku ndipo ndinali otopa... koma utafika pakati pa utsiku, Mulungu anayankhula ndi ine mu mzimu mwanga ndi kundifunsa funso... “Bill, kodi munthu amasunga pati chuma chake cha mtengo wapatali?” Ndinati, “Ambuye, nthawi zambiri chuma ngati golidi, siliva, daimondi, ndi ngale za mtengo wapatali zimtsungidwa pomwe pali potsaonedwa, nthawi zambiri ndi azilonda ndi chitedzo kuti akadzitetedze bwino.”

Mulungu analankhula. “Ngati munthu, chuma changa chamtengo wapatala pa dziko lapansi chatsekeredwa.” Kenako ndinaona Yesa atayimirira pakati pa ndende zochuluka. Ambuye anati, “Asala pang’ono kuwonongedwa ndi satana, koma miyoyoyi iri ndi kuthekera kwakukulu kogwiritsidwa ntchito, ndi kubweretsa ulemerelo ku Dzina langa. Udza anthu anga, ndikupita kundende kukapagitsa kuti mphatso ndi mayitanidwe omwe akungokhala mwa iwo akhale ochitachita. Kuchokera ku ndende izi kuzatuluka ankhondo amphanvu omwe angazakhale ndimphamvu yophwanya zipata za Gehena ndi kugonjetsa mphamvu za satana zomwe zikumanga anthu anga ambiri mu Nyumbwa Mwanga.

“Awuze anthu anga kuti chuma cha mtengo wapatai chiru mkaati mwa ndende, muzida zomwe zayiwalidwa. Anthu Anga akuyenera kubwera ndikukhudza miyoyo iyi, pakuti kudzodzo kwamphamvu kuzamasulidwa pa iwo chifukwa cha chipambano cha mstogolo mu Ufumu Wanga. Akuyenera kubwenzeretsedwa.”

Kenako ndinaona Ambuye atapita pa zipata za ndende ndi fungulo. Fungulo imodzi inatsegula zipata zonse. Kenako ndinamva pokhoso lalikuli ngati khondo. Yesu anati, “Awudze anthu Anga kuti alowe mkaati ndikupulumutsa miyoyo yotayika.” Ndipo Yesu kenako analowa mkaati nayamba kukhudza akayidi omwe amamukanikiza. Ambiri, pokhudzidwa, golide anayamba kumera pa iwo. Mulungu anayankhula ndi ine, “Uyu ndi golide!” Ena siliva anamela pa iwo. Mulungu anati. “Uyo ndi siliva!”

Kenako Ambuye anati. “Ngati anthu anga akufuna kudziwa komwe akufunikira, uwaudze kuti akufunikira m’misewu, m’dzipatala, ndi m’ndende. Akpita kumeneko, akandipedza ine ndi kuyenda kwina kwa Mzimu Woyer.”

# ZOLINGA

Pomaliza pa punziro la bukuli mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kupereka zitsanzo za ulamuliro wa mmalembo wa utumiki wa kundende.
- Kufotokoza chifukwa chimene okhulupirira akuyenera kutengapo gawo pa utumiki waku ndede.
- Kufotokoza zolina za utumiki waku ndende
- Kulemba mndandawa wa zolina za chikhaliwe cha utumiki waku ndende.
- Kulemba mwachidulo zimene Uthenga Wabwino ungapereke ku akaidi.
- Kudziwa ntchito yanu mu utumiki waku ndende.
- Kulemba mwachidule ziyeneretso za uzimu za utumiki wa kundende.
- Kudzindikira dera lokonzekera lofunika pa utumiki wa kundende
- Kulemba mwachidule masitepe oyambitsira utumiki wa kundende.
- Kudzindikira ma utumiki osiyana siyana omwe mungapereke ku ndende.
- Kukonza ndi kupereka pempho la utumiki wa kundende.
- Kulemba ndi kuphunzitsa ogwira ntchito.
- Kufotokodza mene mungayambire kulingana ndi akayidi.
- Kelemba mwachidule malangizo olinganiza ndi akayidi.
- Kufotokoza chifukwa chimene kuyendera akaidi uli utumiki wofunikira.
- Kufotokoza mmene mungatengere gawo mu kuyendera kwa modzi modzi ndi akayidi.
- Kulemba mwachidule malangizo akuyendera kwapanokha ndi akayidi.
- Kudzindikira mitundu yosiyana siyana ya mikumano ya gulu yomwe ingachitike ku ndende.
- Kulemba mwachidule malangizo a kapangidwe ka mikumano ya gulu.
- Kufotokoza chifukwa chimene mabanja a akayidi nthawi zonse amakhala pamavuto.
- Kudzindikira njira zaome mungatumikire mabanja a akayidi.
- Kulemba mwachidule malangizo a kutumikira ku mabanja a akayidi.
- Kufotokoza mmene mungayambire utumiki wa akayidi omwe ali pachigamulo chokanyondegwa.
- Kufofokoza malangizo autumiki wa akayidi omwe akukanyongedwa
- Kufotokoza mmene mungamukonzeretse mkayidi yemwe akukanyongedwa.
- Kudzindikira zosowa za akayidi omwe atulusidwa ku ndende.
- Kufotokoza mitundu ya utumiki wa akayidi omwe atulusidwa kundende.
- Kulemba masitepe poyambisa utumiki wa akayidi omwe atulusidwa ku ndende
- Kudzindikira udindo wanu mu utumiki wa akayidi omwe atulusidwa ku ndende
- Kuonetsera kumvetsetsa chitedzo chakundende.
- Kufotokoza kusiyana kwapakati pa maselo, ndende ndi malo ena osungira akayidi.
- Kufotokoza mitundu ya akayidi.
- Kufotokoza momwe mungagwirire ntchito ndi akayidi omwe akuti sanapalamule.
- Kufotokoza mavalidwe oyenera ku ndende.

- Kufotokoza malamulo za chitedzo za ku ndende.
- Kufotokoza lamulo loyamba popanga ubwenzi ndi akayidi.
- Kulemba machidule malangizo opangira ubwenzi ndi akayidi.
- Kutanthauza “msampha.”
- Kufotokoza mene msampha umachitikira
- Kukamba njira zitata zomwe mungapewere msampha

# **CHAPUTALA 1**

## **“Munadza Kwa Ine...”**

### **Lamulo La M’Baibulo La Utumiki**

**MEVI YOTSOGOLERA:**

**.... ndinali m'nyumba yandende, ndipo munadza kwa Ine. (Mateyu 25:36)**

**ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kupereka zitsanzo za ulamuliro wa mmalembo wa utumiki wa kundende.
- Kufotokoza chifukwa chimene okhulupirira akuyenera kutengapo gawo pa utumiki waku ndede.
- Kufotokoza zolina za utumiki waku ndende
- Kulemba mndandawa wa zolina za chikhalidwe cha utumiki waku ndende.
- Kulemba mwachidulo zimene Uthenga Wabwino ungapereke ku akaidi.
- Kudziwa ntchito yanu mu utumiki waku ndende.

### **CHIYAMBI**

Waya waminga, mipiringidzo ya dzitsulo ndi zitseko zazitsulo zolemera. Nsanja ya olonda ndi alonda omwe ali ndi zida. Zigawenga. Iyi ndi ndende.

-Anthu akuti, “Atsekereni ndipo mutaye fungulo.”

-Andale akuti, “Tikuyenera kumanga ndende zambiri.”

-Chiwerengero chikuti, “80% ya akayidi amabwerera kundende akatulutsidwa--tikutaya nthawi yathu pakuyetsera kuwasintha khalidwe lawo.”

... Koma Yesu anati, “ndinali m'nyumba yandende, ndipo munadza kwa Ine.”

Ndende ndi kachitidwe ka “malonda” kokha kamene kamapindula ndi kulephera kwake. Chiwerengero cha anthu aku ndende chinka nakulira kulirabe. Nthawi zambiri anthu amatuluka mu ndende ali oyipitsitsa kuponsa ndi mmene analowera. Ambiri amachita milandu yambiri, kubwerera ku ndende, ndipo nakhala mu mkombero wa chikhalidwe, “chitseko chongodzungulira” cha milandu, ndende, ndi kutulutsidwa.

Yankho ku izi si ndende zambiri. Tsikutsekera anthu ndi “kutaya fungulo.” Komanso si chilamulo chokanyongedwa, pakuti kafukufuku watsonyedza cuti ngakhale idzi sidzithetsa uchigawenga. Yankho ndi Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu pakuwonetsa mphamvu.

Akayidi akufunika kubadwatso mwatsopano osati kungoyetsera kuwasintha chikhalidwe chawo--ndipo Yesu waperekwa ntchito kwa omutsatira ake kukafikira kupitirira mipanda ya waya wa minga ndi mipiringidzo ya dzitsulo kukakhudza miyoyo ya abale ndi alongo omwe amangidwa ndi nsinga za tchimo.

### **ULAMULIRO WA UTUMIKI WA KUNDENDE**

Ulamuliwa wa utumiki waku ndende ulukuonetseredwa mu Mawu a Mulungu, pakudzera mu malembo ndi zitsanzo.

#### **MALEMBO:**

Lamulo lalikulu la utumiki waku ndende laperekedwa pa Mateyu 25:31-40. Yesu anati:

... “Koma pamene Mwana wa munthu adzadza mu ulemerero wace, ndi angelo onse pamodzi naye, pomwepo Iye adzakhala pa cimpando ca kuwala kwace: ndipo adzasonkhanidwa pamaso pace anthu a mitundu yonse; ndipo Iye adzalekanitsa iwo wina ndi mnzace, monga mbusa alekanitsa nkhosa ndi mbuzi; nadzakhalitsa nkhosa ku dzanja lace lamanja, koma mbuzi kulamanzere. Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lace lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa cikhazikiro cace ca dziko lapansi: pakuti ndinali ndi njala, ndipo munandipatsa Ine kudya; ndinali ndi ludzu, ndipo munandimwetsa Ine; ndinali mlendo, ndipo munacereza Ine; wamarisece Ine, ndipo munandibveka; ndinadwala, ndipo munadza kuceza ndi Ine; ndinali m'nyumba yandende, ndipo munadza kwa Ine. Pomwepo olungama adzamyankha Iye kuti, Ambuye, tinakuonani Inu liti wanjala, ndi kukudyetsani? kapena waludzu, ndi kukumwetsani? Ndipo tinaona Inu liti mlendo, ndi kukucerezani? kapena wamarisece, ndi kukubvekani? Ndipo tinakuonani Inu liti wodwala, kapena m'nyumba yandende, ndipo tinadza kwa Inu? Ndipo Mfumuyo idzayankha nidzati kwa iwo, Indetu ndinena kwa inu, Cifukwa munacitira ici mmodzi wa abale anga, ngakhale ang'onong'ono awa, munandicitira ici Ine.” (Mateyu 25:31-40)

#### **CHITSANZO:**

Yesu mwini ndi chitsanzo chathu cha utumiki waku ndende. Mbali yina imene Yesu amakatumikira kunali ku ndende:

... **Kuti utsegule maso akhunu, uturutse am'nsinga m'ndende, ndi iwo amene akhala mumdimba, aturu ke m'nyumba ya kaidi.** (Yesaya 42:7)

Yesu analengedza:

“**Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine; pakuti Yehova wandidzoza ine ndilalikire mau abwino kwa ofatsa; Iye wanditumiza ndikamange osweka mtima, ndikalalikire kwa am'nsinga mamasulidwe, ndi kwa omangidwakutsegulidwa kwa m'ndende**” ... (Yesaya 61:1)

Ngakhale pamene amafa pa ntanda wa Kavale, Yesu anantenga nthawi mwachikondi kufikira mkaidi. Padotsatira, chigawenga chomandidwa chinakumana ndi chikondi cha Mulungu, chisomo, ndi kukhululikidwa kwa machimo. Pakati pa nthawi ya kufa ndi kuuka kwake, timaudzidwa kuti Yesu “...m'menemonso anapita, nalalikira mizimu inali m'ndende” (1 Petro 3:19).

Mwatsoka, ngakhale mu Baibulo muli lamulo komanso zitsanzo za Yesu kutumikira kwa akayidi, okhuluporora ambiri amakonda kungodutsa m'mbali yina ya njira, ngati mmene anachitira adzitsogoleri a chipembedzo mu fanizo la Msamaliya Wachifundo (onani Luka 10:29-37).

### **CHIFUKWA CHANI UTUMIKI WAKU NDEDE?**

Ndichifukwa chani okhulupirira akuyenera khudzidwa ndi utumiki wa kundende? Chifukwa...

1. Chifukwa utumiki waku ndende uli ndi ulamuliro wa malembo (Mateyu 25:31-40). Mu Baibulo monse muli zitsanzo, kafotokodzeredwe, ndi malamulo a ndende, akayidi, omangidwa, ogwidwa, ndi ukapolo. Baibulo linakamba za ndende, akayidi, kapena kumangidwa kopitilira ka 130. (Onani Zakumapeto 2 za bukuli)
2. Tiuyenera kutsatira chitsanzo chomwe Yesu anayika pakutumikira a mndende.
3. Ndende zimafikira muyeso wa malo onse otumikirako: Anthu otayika ndi kufunika kwa ogwira ntchito.
4. Mulungu sakufuna kuti wina aliyense atayike--ingakhale zigawenga, ogwiririra, kapena ambanda (2 Peter 3:9). Mulungu amakonda ingakhale munthu “wochimwitsitsa” (1 Timoteo 1:15).
5. Azibusa akundende sangatumikira oposa omwe anapatsidwa kuti adziwasamalira. Sanachite ntchito yonse yomwe ikufunikira okha, pakuti palibe nthawi yokwanira yochitira idzi.
6. Ndende zambiri ziribe azibusa odziwa bwino ntchito yawo ndipo zilibi misonkhano ya chipembedzo.
7. Munthu wina aliyense wamangidwa, pali anthu ambiri omwe amakhudzidwa: akayidi, ana, makolo, ndi ena ambiri. Akayidi ndi mabanja awo amayimira gawo lalikula la anthu mu mtundu wina uliwonse.
8. Dzipembedzo zonyenga ndi amatsenga akufikira a ndende. Tikuyenera kukafikako mwachang ndi Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu!

### **ZOLINGA ZA UTUMIKI WAKU NDENDE**

Zolina za uzimu za utumiki waku ndende utha kukhala ndi zolina ngati zotsatirazi:

- Kugawa chikondi chopanda mangawa cha Mulungu
- Kukapereka Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu mu nira yoti upangitse akayidi kuwulandira ndi kuvomeredza Yesu ngati Mpulumutsi
- Kukaphunzitsa okhulupirira atsopano Mawu ndi kuwaphunzitsa mmene angamawerengere Baibulo.
- Kukaonetsera mphamu ya pemphero ndi kuwaphunzitsa kupemphera.

- Kuwatengera akayidi kuti akakumane ndi mphamvu ya Mulungu yotsintha moyo yomwe ingawamatsure kuti maganidzo odzimvera chitsoni kuti iwo ndi wolakwa, manyazi, ndi maganizo otsakhala bwino, ndi zilakolako za zinthu zoyipa.
- Kutumikira mabanja a akayidi.
- kuthandiza akayidi kukhala moyowabwino.
- kupereka chithandidzo kwa akayidi omwe atuluka ku ndende.

### **CHOMWE UTHENGA WABWINO UMAPEREKA KWA AKAYIDI**

Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu uli ndi zinthu zambiri zopereka kwa akayidi.

- Kukhululukidwa kwa machimo.
- Mwayi onena kuti “pepani”
- Kumasulidwa kuchokera ku ukapolo ndi chitonzo.
- Kulandiridwa--pamene ambiri ayiwo chomwe akudziwa ndi kukanidwa.
- Makhalidwe ndi kachitidwe ka zinthu katsopano
- Njira zothanira ndi nyengo zovuta ndi maganizo olakwika.
- Moyo wochulukwa kudzera mwa Yesu Khristu.
- Cholina chatsopano cha moyo.
- Moyo wosatha.

### **KODI UDINDO WANU NDI WOTANI?**

Pa a Khristu ochuluka a dziko lapansi, ndi ochepta okha omwe amapanga utumiki waku ndende, ingakhale ndende zimapezeka kumadera ambiri.

Okhulupirira wina aliyense akuyenera kutengapo gawo pa utumiki waku ndende. Idzi sizikutanthauza kuti munaitanidwa ku utumiki waku ndende. Ngati mu utumiki--siwina aliyense yemwe anaitanidwa kupita ku mayiko ena kukagawa Uthenga Wabwino. Koma---mu utumiki--okhulupirira wianaliyense akuyenera kutengapo gawo pa utumiki wa ku ndende.

Pali njira zambiri zotengerapo gawo:

- Kupempherera omwe akuchita utumiki wa ku ndende.
- Kuyendera akayidi.
- Kulembra akayidi.
- kuthandidza mabanja a akayidi.
- Kuthandidza akayidi kuti akhale ndi moyo wabwino akatulutsidwa ku ndende.
- Kupanga mapemphero, Kusanthura Baibulo, kapena mikumano ya m’magulu ku ndende.
- Kulemba, kufalitsa, ndi kugawa zinthu zothandidzira maphunziro a Baibulo a akayidi aku ndende.
- Kupereka ma Baibulo ndi mabuku achi Khristu kwa akayidi.
- Kupereka chithansidzo cha chuma kwa iwo akuchita utumiki wa kundende.
- Kugwira ntchito ngati m’busa waku ndende.

Yambani kupemphera pano kuti Mulungu akubvumbulutsireni njira zomwe mungatengerepo gawo!

### **Chiyambi Chatsopano**

“Ine ndine mkayidi owerudzidwa, ogamulidwa kukafa ku ndende. Ndaphunzira kuti pamene ukumva kuti wataya zonse, Mulungu amakuonetsera kuti walandira zoponsa zomwe dziko langathe kupereka.

“Ndende ndi malo omwe Mulungu angatipange kukhala zida zofunikira zomwe zingakhale nthawi yambiri ya kulambira ndi matamando, kaya tikugwira ukayidi wa miyezi isanu ndi umodzi kaya wa moyo wathu onse. Mochuluku ndikuwerenga Baibulo, ndimochuluka ndikukhumba kumudziwa Mulungu. Mochuluka ndikukhala ku ndende, ndi mochuluka ndikufuna kukhala chifupi ndi anthu omwe amakhala moyo wa Mulungu ndi kulambira nawo limodzi. Ndende ndi maloomwe Ambuye athu kuchita ntchito zina zake zabwino.

“Ndende sizikuyenera kukhala mathero a moyo. Zitha kukhala chiyambi chatsopano, ngakhale yemwe akugwira mulandu wa moyo wake wonse.” (RS)

## **MAFUNSO OZIYETSA NOKHA A CHAPUTALA 1**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Perekani zitsanzo za ulamuliro wa mmalembo za utumiki wa kundende.

---

3. Kodi ndi ndani yemwe ali chitsanzo chathu chachikulu m'Baibulo pa utumiki wa kundende?

---

4. Lembani zolina zisanu ndi zitatu za utumiki waku ndende

---

---

5. Kodi zolina za uzimu za utumiku waku ndende ndi ziti?

---

6. Lembani mwachidulo zimene Uthenga Wabwino ungapereke ku akaidi.

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 2**

## **Ziyeneretso Ndi Kukonzekera**

### **VESI YOTSOGOLERA:**

**... komatu khala citsanzo kwa iwo okhulupira, m'mau, m'mayendedwe, m'cikondi, m'cikhulupiriro, m'kuyera mtima. (1 Timoteo 4:12)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba mwachidule ziyeneretso za uzimu za utumiki wa kundende.
- Kudzindikira dera lokonzekera lofunika pa utumiki wa kundende

### **CHIYAMBI**

Iwo omwe akutumikira utumiki wa kundende akhale kuti akutsimikizika za ubale wawo ndi Khristu, khalani chitsanzo chabwino, nthawi zonse mukhale okonzeka kupereka yankho ya chiyembekezo mkatи mwawo. Pamene mutnhu yemwe wayitanidwa ku utumiki akuyenera kuwometsera makhalidwe auzimu ophunzitsidwa mu Mawu, chaputala ichi chikukamba za ziyeneretso zofunikira zomwe ogwira ntchito ku ndende ayenera kuhala nazo.

### **ZIYENERETSO ZA UZIMU**

### **KULIMBA MTIMA:**

Kulowa mu tumiki wa kundende--kaya ndi utumiki wokumana ndi munthu m'modzi m'modzi kapena kukumana ndi gulu--ndi kunja kwa malo zhitetedzo kwa okhulupirira ambiri. Ndidsotsakayikitsa kuhala ndi mantha matsiku oyembirira kulowa ku ndende--koma dzindikirani, Mulungu adzakutsamalirani pamene mukugwira ntchito yake. Mu nyengo zambiri, malo opemphereramo aku ndende ndi malo abwino kukumaniranako ndi akayidi chifukwa akayidi amakhalamo momasuka komanso amsangala. Ngati muli ndi matha, kumbukirani kuti Mulungu sapereka mzimu wamantha--ndiye dzindikirani komwe mantha amachokera ndipo agonjetseni.

### **MGIRIZANO:**

Pali anthu osiyana siyana ku malo a ndende. Ngati ogwira ntchito yongothandidza--kuphatikidza pa akayidi mudzikumana ndi anthu ogwira ntchito ku ndende (otchedwanso azilonda) ndi m'busa wa kundende. Anthu ambiri omwe mungakumane nawo akusamalani mwa ulemu. Inunso onetsetsani kuti muwapase uleme, kulankhulana nawo ndi kugwirana nawo chanza pamene pakufunikira, kugwiritsa ntchito mayina awo ngati kuli koyenera kutero. Ogwira ntchito ku ndende wabwino amadziwa momwe angagwirizanire ndi anthu ena.

Ndikofunikira kwa inu, ngati ogwira ntchito modzipereka, kumvetsetsa ntchito ya m'busa ya m'busa wa kundende. Azibusaaku ndende amagwira ntchito ma ola ambiri komanso mu nyengo

zobvuta. Tsiku ndi tsiku m'busa wa kundende amakumana ndi maudindo othana ndi mabvuto a akayidi, kupereka ma pologalamu okumana ndi zokhumba za uzimu za akayidi, kulimbana ndi kukhumudwitsika koma kumakhala kukuchitika nthawi ndi nthawi.

M'busa amagwira ntchito ngati wamkulu ma chipembezo ku ndende. Iye amaperea ulaliki ndi zochitika za chipembedzo, kuyang'anira maphunziro achipembedzo; nthawi zambiri amakhala akupereka chilangidzo kwa akayidi, kulemba, ndi kuphunzitsa ogwira ntchito odzipereka; ndi kuchita ntchito zina zambiri zotukula umoyo pa mu ndende.

Ndi zofunikira kuti ogwira ntchito yongodzipereka adzikhala pa ubale wabwino ndi azibusa aku ndende. Ndikulakwitsa kwakukulu kugwiritsa ntchito mwayi wanu okatumikira kundende kuti mukayipitse mbiri ya m'busa wa kundende ndi kunyozetsa ntchito yake. Ngati pali vuto, nthawi zonse yankhulanani ndi abusa aku ndende nusanalankhulane ndi munthu wina.

### **CHENICHENI:**

Khalani oona mtima! Akayidi ndi aluso podzindikira chinthu chomwe sichirichenicheni. Munthu asapite kundende ndi zolina zolakwika ngati kukapeza mabanja, kapena kukadzionetsera kuthekera kwake. Akayidi amadzindikira mwachangu omwe akupanga utumiki wa ku ndende omwe ali ndi zolina zolakwika. Zolina zozikonda nokha ndi makhalidwe ofuna kudzionetsa kuti inu ndiye oyera mtima kwambiri kuponsa onse alibe mbali mu utumika wa kundende.

### **KUDZICHEPETS:**

Khalani ndi mtima wodzichepetsa. Dzindikirani, kuti inu muli kumeneko kuti mukathandidze. Khalani odzicheoetsa kwa iwo omwe ali ndi maudindo awo (azibusa, azilonda).

### **KUKHULULUKA:**

Limbikitsani mzimu okhululuka, dzindikirani kuti kupanda chisomo cha Mulungu inu munakatha kuhala ngati iwo. Dzindikirani kuti chikhululuko cha Mulungu chimafikira anthu onse omwe amatengedwa ngati otayika mmaso mwa anthu.

### **KUPIRIRA:**

Anthu ambiri atayachikhulupiriro pa akayidi. Iwo sakufuna wina kuti awakane. Khalani odekha mtima. Mulungu walonjedza kuti inu mudzatuta zokolola za uzimu mu nyengo yake. Ogwira ntchito ya utumiki wa kundende omwe amayamba utumiki ndi kulekedza panjira amachotsa chidwi cha akayidi, kukhumuditsa azibusa ndi ogwira ntchito ku ndende, ndikupereka chithunzithunzi choyipa ku mpigo.

### **KUKHULUPIRIKA:**

Khalani okhulupirika ndi okhazikika pogwira ntchito yanu, makamaka pakutsunga malonjezano ndi kupeze ka mu nthawi yake yoyikika. Azibusa akundende amadalila inu, chomwechonso akayidi. Kuyendera akayidi komwe ndi chimodzi cha ma pologalamu anu a patsiku ndi chinthu cha mtengo wapatala kwa akayidi. Otsawakhumudwitsa. Khalani okhulupirika ku ntchito imene Mulungu wakudalirani nayo.

## **CHIFUNDO:**

Chifundo ndi kuthekera komva zomwe anthu akumva ngati kuti inu muli mmalo awo. Mu Chipangano Chakale, Mneneri Ezekieli anakhala limodzi ndi ogwidwa m'mbali mwa Nsinje wa Kaba atsanayambe kugawana nawo uthenga. Analu okonzeka kumvetsera, chifukwa amadziwakuti iye amamvetsetsa nyengo zawo. Iye “anakhala pomwe iwo anakhala” (Ezekiel 1:1)

## **MALINGALIRO A UTUMIKI:**

Malingaliro a utumiki ndi kukhumba kwa mtima kupereka ku utumiki kakhala woyambirira pa zonse (pa nthawi yomwe wayikidwapo), kukhulupirira kuti utumiki ndi zomwe mukunera kuchita kupatula china chiri chonse.

## **KUKULA MU UZIMU**

Inu mutsamangotsogorera akayidi ku kukula kwatsopano muuzimu, koma mukhale ndi chidwi chokula mu uzimu. kukula mu uzimu ndi zinthu za moyo wonse. Ngati mukuzinva kuti inu “mwafikapo” kaya mu chidziwitso kapena chikhaliwe, inu mukungoonetsera umwana wanu.

## **CHIKONDI:**

Werengani 1 Akorinto 13. Mphamu yachirimbikitso chachikulu pa utumiki, makamaka wa kundende, ndi chikondi. Chikondi pa Mulungu. Chikondi chosaona nkhope pa akayidi. Chikondi cha utumiki womwe Mulungu wakuyitanirani.

## **KUKONZEKERA**

Pali mbali zinayi zofunikira kukonzekera kwa iwo akukhumba kupanga utumiki wa kundende:

### **1. KUKINZEKERA MU PEMPHERO**

Ngati utumiki wana uli onse, pemphero ndi lofunika kwambiri kuti utumiki ukakhale opindura. Zawo magawo omwe mukuyenera kupempherera:

- M'busa wa kundende.
- Akayidi onse.
- Mabanja a akayidi.
- Ogwira ntchito ku ndende.
- Chitedzo cha anthu otumikikira.
- Chidziwitso choti akafikire zokhumba za akayidi.
- Chitsitsimutso cha uzimu.
- Kuti Mulungu adzutse adzitsogoleri ampham. vu pakati pa mpingo waku ndende.
- Zopempherera za akayidi. Makachisi amabiri akaundende amakhala ndi bokosi yoyikamo zopempherera. Akayidi amalemba zopempherera zawo naziyika mu bokosilo kuti abusa ndi otumikira akazipempherere.

## **2. KUKONZEKERA MU MAWU**

Ogwira ntchito ya utumiki wa kundende akuyenera kukhala ndi chidziwitso chogwira ntchito cha Baibulo ndi mfundo za chi Khristu. Akayidi ambiri sachita chidwi ndi mfundo za bwino, koma amafuna kaperekedwe ka bwino aka uthenga wabwino. Ngati simuwerenga ndi kumvetsetsa Mawu, kodi mungathandidze bwanji wina kuti aphonzire ndi kumvetsetsa Baibulo? Kuti mukhale ogwira ntchito wabwino, mukuyenere kuti mudziwerernga Mawu a Mulungu nthawi zonse.

## **3. KUKONZEKERA PA MA UDINDO ANU**

Konzekani pa mauzindo anu a utumiki. Ngati mukukayimba, onetsetsani kuti zida zonse zoyimbira ziri bwino. Ngati mungakaphunzutse, tengani nthawi yokwanira yokonzekera chipheunzitso chani.

## **4. KUKONZEKERA ZA MALO OMWE MUKUPITAKO**

Zikonzekeretseni nokha malingana ndi kumalo komwe mukupitako:

- Dzindikirani malamulo akavalidwe ndi kachitidwe ka zinthu za kundende kmwe mukukatumikira. Izi zimakhala zosiyana siyana malingana ndi ulamuliro wa ndende.
- Dzindikirani momwe ulamuliro umayendera, amene mukuyenera kukumana naye ngati otumikira.
- Dzindikirani zomwe mukuyenera kutinga mukamalowa mu ndende.
- Khalani ndi chidziwitso cha mmene utumiki wovomeredzedwa wa Chikhritsu ukachitikire mu ndende.
- Khalani nawoni pa mitsonkhanu yomwe amachititsa azibusu aku ndende.

## Mkazi Womangidwa Yolembedwa ndi Kessie Logan

Nthawi zina ndi malo awekha,  
Palibe okondedwa yemwe amapedzeka,  
Kufunafuna kwa chimwemwe cha mkati,  
Koma nkhwawa zimakumanga,  
Pomwe ndakhala pansi ndikumayang'ana kunja kwa  
mpanda,  
Magalimoto akudutsa,  
Kudabwitsika kwa idzo,  
Zimandipangitsa kuti ndi yimwe ndikudzifutsa kuti  
“chifukwa chani?”  
Kodi Mulungu wayiikidza chani pa ine,  
Mtamda uwu wodabwitsa kuti ndinyamule?  
Ndichifukwa chani Mulungu wachikondi yemwe  
ndimamutumikira,  
Akavomeredze zosakhala bwino?  
Nthawi kwa ine siyatsopano,  
Ndivomereze malingana mmene ndingathere,  
Pakuti ndikudziwa kuti mudzochitika za zinthu,  
Yesu wanga ali ndi pulani,  
Ndipo tsiku lina, ndidzatuluka muno,  
Pmene mawu a Ambuye adzayitane,  
Ndipo ndidzakamba nkhanji yanga,  
Ya “mkazi womangidwa.”

## **MAYESO OZIYETSA NOKHA A CHAPUTALA 2**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Lembani mwachidule ziyeneretso za uzimu za utumiki wa kundende zomwe zafotokodzedwa mu chaputalachi.

---

---

---

3. Dzindikirani madera anayi onzekera ofunika pa utumiki wa kundende

---

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 3**

## **Kuyamba Utumiki Wa Kundende**

### **VESI YOTSOGOLERA:**

**Koma awa ndiwo anthu olandidwa zao ndi kufunkhidwa; iwo onse agwa m'mauna, nabisisidwa m'nyumba zakaidi; alandidwa zao, palibe wowapulumutsa; afunkhidwa ndipo palibe woti, Bwezerani. (Yesaya 42:22)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba mwachidule masitepe oyambitsira utumiki wa kundende.
- Kudzindikira ma utumiki osiyana siyana omwe mungapereke ku ndende.
- Kukonza ndi kupereka pempho la utumiki wa kundende.
- Kulemba ndi kuphunzitsa ogwira ntchito.

### **CHIYAMBI**

Inu mwatsimikizika mtima. Malamulo ndi zitsanzo za m'Baibulo zawonet sedwa poyer. Ngati okhulupirira, mukufuna kutengapo gawo pa utumiki wa kundende. Koma muyamba bwanji? Kodi mupeza bwanji njira yaku ndende? Chaputala ichi chikukamba masitepe oyambitsira utumiki wa ku ndende. Mumphunzira mitundu yosiyana siyana ya mautumiki omwe mungayambitse ku ndende, momwe mungalembere ndi kupereka pempho la pologalamu yanu, ndi njira zolembera ndi kuphunzitsira ogwira ntchito.

### **KUYAMBA UTUMIKI WA KUNDENDE**

Idzi ndi masitepe asanu ndi awiri omwe angakuthandidzeni uyamba utumikiwa kundende.

### **SITEPE YOYAMBA: Pephero**

Zinthu zonse zimapasidwa mphamu ndi pemphero. Pemphereani zimene Mulungu akufuna pa ndi udindo wanu mu izo. Ikani madziko apemphero musanayambe utumiki wanu.

### **SITEPE YACHIWIRI: Kakumaneni ndi atsogoleri anu a uzimu**

Ngati ndinu m'busa, kakumaneni ndi oyang'anira mpingo wanu wonse. Ngati muli membala wa mpingo, kakumaneni ndi abusa anu. Izi ndi zofunika pazifukwa zambiri:

- Ndi dongosolo yokhazikika.
- Adzitsogoleri auzimu atha kukutsogorerani ndi kupereka nzeru zofunika.
- Adzitsogoleri anu atha kukhala kuti anali kale ndi mapulani a utumiki umenewu. Ngati ziri choncho, khalani mbali ya utumikiwo, osauyang'anira pansi.

Yetsetsani kupeza chirimbikitso kuchokera kwa abusa anu kapena adzitsogoreri anu auzimu. Chirimbikitsochi ndichofunikira kuti mupeze anthu okuthandidzani pa utumiki. Chinsisi

ndikuwaonetsa abusa anu momwe utumiki wanu ungagwirizane ndi mapologalamu, mautumiki ndi zochitika zina zapa mpingo.

### **SITEPE YACHITATU: Pangani kafukufuku**

Awa ndi mafunso omwe mukuyenera kuyankha pomwe mukupanga kafukufuuku:

-Kodi ndi ndende ziti mwayandikana nazo?

-Kodi mudera lanu muli utumiki? Kodi akupanga chani? Kodi ali ndi chidwi ndi utumiki wa kundende? (ngati ali kale ndi utumiki wa kundende, mhiwina mungaganize zochina nawo limodzi)

-Kodi amene ali oyang'anira ogwira ntchito za chifundo ku ndende ndi ndani? Lumikizanani nawo ndi kupeza:

-Kodi chiroledzo chotumikira ku ndende chimapezeka bwanji?

-Kodi pali pali ma fomu omwe mukuyenera kulembapo?

-Kodi pali maphunziro apaderadera omwe mukuyenera kuphunzira?

-Kodi ndi chidzindikiritso chotani chomwe mumuyenera kukhala nacho kuti mukaloledwe kulowa mu ndende?

-Kodi ndizosowa zanji zomwe ziripo mu ndende zawo?

-Kodi ndizosowa zanji zomwe inu ndi/kapena mpingo wanu mungakwanitse kupereka? Muyetsetse kuti musachite zinthu zomwe anthu ena akuchita kale. Tikuyenera kuyamikirana, osati kuchita mpikisano.

-Zochitika zomwe mungathe kupereka ku ndende ndi:

-Kuchititsa mapemphero.

-Kugwira ntchito ya abusa aku ndende pamene adwala kapena ali ku tchuthi.

-Kupereka mapologalamu a machimbidwe kapena zisuzo apaderadera.

-Kuchita ma pologalamu osanthula Baibulo.

-Kupereka ma Baibulo.

-Kuonetsa kanema wa uzimu.

-Chitani ma pologalamu okumana ndi m'modzi m'modzi

-Perekani maphunziro a Baibulo.

*Zindikirani: Musananayambe kulemba pempho lanu, muwerenge Chaputala 4-9 a bukuli omwe akukamba za mautumiki osiyana siyana omwe inu mungakhumbe kutengapo gawo.*

### **SITEPE YACHINAYI: Kukonza pologalamu la pempho**

Pempho li...

-Fotokoza zolina ndi magwiridwe a ntchito a pologalamu yanu.

-Maperekedwa kuti likamvomerezewa ku ndene komwe mukufuna mukachiteko utumiki.

-Magwiritsidwa ntchito ngati chida zolembera anthu ogwira ntchito. (Mukuyenera kuziwa mtundu wa utumiki womwe mukufuna kuchita kuti mukalembe ntchito anthu oyenerera.)

Pemphe lanu likuyenera kuona zinthu izi:

**Zolina:** Kodi cholina cha pologalamu yanu ndi chani? Kodi mukufuna kukwanirisa chani? Onani Chapatala 1 cha bukuli pomwe pali mndandanda wa zolina. Muonetsetse kuti muli ndi zolina zanu zapaderadera.

**Phindu:** Kodi pologalamu yanu ipindulira bwanji akayidi? Kodi ipundulira bwanji ndende yonse?

**Wotsogorera:** Kodi amene adzitsogolera pologalamu yanu ndi ndani? Kodi zomuyenereza zake ndi chani?

**Ogwira ntchito:** Kodi ndi ndani yemwe adzitengapo gawo pa pologalamu yanu? Kodi ndi maphunziro otani omwe angalandire? (Mutha kugwiritsa ntchito bukuli pochitsa maphunziro. Chimenecho ndi cholina chimene bukuli linalembewera)

**Malo ochitira utumiki:** Ndi malo otani omwe mungafune kuti muzichitira utumiki? Kodi mukufuna muzigwiritsa kachisi ya kundende? Kapena malo ena okumanirana ndi anthu?

**Masiku, nthawi:** Masiku ndi nthawi yomwe mungafuni kumakumana.

**Zida:** Kodi mufuna zida ngati ma polojejita, zida zanyimbo, mabuku a nyimbo? Kodi zinthuzi ndi zoti ndende ikupereka kapena mubera nazo zanu? Kodi ndende ilola kuti muzilowese mkati mwa ndende?

**Zachuma:** Ingakhale utumiki wa kundende umachitika ndi anthu ongoziperek, koma patha kukhala zinthu zomwe zingafune ndalama. Mwa chitsanzo, ngati mukufuna kukagawa ma Baibulo, mabuku, kapena zinthu zina zopereka zomwe zavomerezeza ndi aku ndende.

Ku ndende komwe mukufuna kukatumikira atha kukhala ndi fomu yoti mutsatire pomwe mukulemba pempho lanu. Funsani za izi. Yotsatirayi zi chitsanzo cha fomu la pempho lomwe limagwiritsidwa ntchito ku ndende ina ku United States:

### **Fomu Ya Chitsanzo**

1. Kodi pologalamu yanu idzidzayendetsedwa ndi nadani?
2. Kodi angadzakhale ndi udindo wa pologalamu yanu ndi ndani?
3. Kodi zolina za pologalamu yanuu ndi ziti?
4. Kodi pologalamu yanu idzapereka ntchito yanji kwa akayidi?
5. Kodi pologlamu yanu idzidzapereka ntchito zanji ku ndende?
6. Kodi pologalamu yanu idzaperekedwa pa njira yanji?
7. Kodi woyendetsa pologalamu yanu ali ndi maphunziro otani?
8. Kodi pologalamu ya ulendo idzayendetsedwa bwanji?
9. Kodi pologalamu yanu idzidzakumana matsiku/malola angati?
10. Kodi ndi anthu angati omwe akutengapo gawo pa pologalamu yanu?
11. Kodi aphunzitsidwa bwanji?
12. Kodi ndi malo aakulu bwanji adzafunikire pa mkumano wanu?

Uthenga wotsatirawu ndiwofunikira pa munthu wina aliyense amene mukufuna mumubweretse ku ndende:

- 1) Dzina
- 2) Tsiku lobadwa
- 3) Chiphatso choyendetsera galimoto
- 4) Numbala cha chitedzo

Chonde tipatseni ife zitsanzo za kugwira ntchito kwanu ndi ndende mbuyomo ndi/kapena uthenga wina uli wonse womwe ukuonetsera kutsiyana kwa utumiki wanu ndi mautumiki ena.

Yotsatirayi ndi kalata ya chitsanzo yogwiritsidza polemba pempho ku ndende:

## Adiresi Yanu

Tsiku  
Adiresi yawo

Wokondedwa

Tikupempha chiroledzo chozapanga utumiki wa kundende ku (dzina la ndende).

Pologalamu yathu ikukhuzana ndi akayidi, koma tikukhulupirira kuti ikathandidziratso ogwira ntchito pakuwapatsa akayidi mwayi ogwiritsa ntchito bwino nthawi yomwe amakhala kuti alibe zochita ndi kukweza makhaldwe a akayidi. Komatso zikuonetsera kuti akayidi amene amakhala pansi pa chipunzitso cha Baibulo limaphunzitsa amakhala nzika zabwina za dziko.

Ogwira nchito athu adzaphunzitsidwa maphunziro akundende, komwe tingadzawaphunzitse malamulo akavalidwe ndi chitedzo, mituntu ya ndende ndi akayidi, ndi momwe angapangire ubwenzi ndi akayidi. Mu maphunziro athu, kutsindikidza kumayikidwa pakudzindikira ndi kulimbikitsa malamulo ndi kupewa mavuto. Koma, nagti kungafunikire, tidzakondwera kuphunzitsidwa ndi ogwira ntchito anu.

Pa nthawi ino, tiri okonzeka kupereka mapologalamu otsatirawa: (Fotokodzani mwatsatane tsatane pologalamu omwe mukuyembekedzera kudzapereka, kkugwiritsa ntchito malangidzo omwe aperekedwa mu chaputala ichi).

Ndikuyembekedzera kulankhulana nanu pamanso ndi pamanso zokhudzana ndi pempho iri. Dzikomo chifukwa cha nthawi yanu ndi kuvomeredza kwanu kwa pempholi.

Landirani ulemu wanu,  
(Dzina lanu)

Ngati munachitapo utumiki wa kundende kwina kwake, phatikidzani kalata yochokera kumene munachitako utumiki poyamba. Ngati munalandira pempho kuchokera kwa akayidi ku ndende lokhudzana ndi pologalamu yomwe ikupereka, phatikizani izi pa pempho lanu.

## SITEPE YACHISANU: Kupereka pempho lanu

Perekani pempho lanu kwa abusa anu kapena atsogoreri anu auzimu kuti ayiunike kaye, kenako katsiyeni pempho lanu ku akuluakulu aku ndende ndipo dikirirani yankho lawo. Atha kukuyitanani kuti mukakumane nawo ndi kukambirana za pempho lanu. Ngati ziri chonco, kafikeni mu nthawi yake, mutavala bwino, komanso okonzeka bwino. Ngati simunalandire yakho lin lirironse kuchokera kw akulu akuluaku ndende mutakasiya pempho lanu patapita kanthawi, mutha kuwayimbila foni ndikupempha kuti mukumane nawo.

Ngati pempho lanu lakanidwa, yetsanitso patatha, miyezi ingapo. Uku kutha kukhala kukuyesani ngati muli odzipereka ndi odikira.

### **SITEPE YACHISANU NDI CHIMODZI: Lembani ndi kuphunzitsa ogwira ntchito**

Pakutha pa kuvomerezewa kwa pempho lanu ndi abusa anu komanso akuluakulu aku ndende komwe mukufuna kukachita utumiki, mukufunikira kulemba ogwira ntchito. Ogwira nchito ndiofunikira...

-**kwa akayidi**, ngati njira ya kunja kwa ndende, m'nesi, komanso chitsanzo cha moyo wa chikhristu.

-**kwa mabanja a akayidi**, amapereka uthenga komanso chithandidzo chauzimu pamene akukhala mu moyo wovuta.

-**kwa m'busa**, pakuthandiza mapologalamu ake.

-**Ku utsogoleri wa kundende**, ogwira ntchito atha kupereka chithanidzo chomwe akulu akulu andende sangakwanitse kupereka.

**Kwa ogwira ntchito ena**, ngati gwero lachilimbikitso, maphunziro, ndi chitsanzo chochitsatira.

-**kumpingo wa mdera lawo**, ngati njira yoperekera uthenga, kupititsa patsogolo chidziwitso cha kufunikira kwa utumiki wa kundende.

-**kwa iye mwini**, pomwe utumikiwu umapereka mwayi oti agwirtse ntchito mphatso zake za uzimu ndi chikhulupiriro chake.

Pali njira zambiri zopedzera ogwira ntchito mogodzipereka:

-Ikani chidziwitso ku mpingo.

-Lengedzani mu mpingo.

-Pangani maposita ndikuwamata m'malo ofunikira mu mpingo wanu.

-Chitani "Tsiku la Utumiki wa ku ndende" mu mpingo kapena mipinggo yomwe mukufuna itengepo gawo pa utumiki waku ndende. Olankhula akhale yemwe ali wochita chita pa utumiki wa kundende ndi kuika ma umbondi a anthu omwe anali akayidi.

Lengedzani ma pologalamu omwe muli nawo ndi kuyitanitsa msonkhano wa anthu omwe awonetsa chidwi chofuna kupanga nawo utumiki wa kundende.

Pamene mukuona mosamala ogwira ntchito amene mukufuna muwalembe ntchito, lingalirani zotsatirazi:

-Kodi munthuyo anachitapo utumiki wa ku ndende?

-Kodi munthuyu ali ndi luso la mayimbidwe?

-Kodi amalankhula zilankho zingati?

-Kodi ali ndi kuthekera kotsogorera gulo laling'ono?

-Kodi mphatso zaho za uzimu ndi ziti? Mphatso za chipunzitso ndi kupereka malangidzo ndi mphatso zofunikira kwambiri.

- Kodi anamangidwapo? Ngati ziri choncho, onani ngati angalorezedwe kukalowa ku ndende.
- Dzindikirani gawo limene angakwanitse kugwira ntchito bwino:
- Kulembra akayidi?
- Kukumana ndi akayidi?
- Kutumikira ku mabanja a akayidi?
- Utumiki mwa m'magulu ku ndende?
- Utumiki wa akayidi omwe atulutsidwa?

Ogwira ntchito akuyenera kulemba mu fomu pa mkumano wanu woyamba. Mutha kugwiritsa ntchito mofu yomwe iri mutsiyi ngati chitsanzo:

**Mafunso a Anthu Ogwira Ntchito**  
(zolemba zonse zikuyenera kutsungidwa pamalo achinsisi)

Dzina \_\_\_\_\_ Dzaka \_\_\_\_\_

## Mwamuna/Mkazi

**Adresi**

Mzinda wanu\_

Lamyia (\_\_\_\_) \_\_\_\_\_ Ndinu okwatira: \_\_\_ Si

\_\_\_\_ Muli pa banja

## Ntchito yomwe mum

Lamya ( )

Ndinu membala wa mpingo wanji?

Uli ku: \_\_\_\_\_

CH RA: \_\_\_\_\_

Chonde onani dera la ndende lomwe mukufuna kukachitako utumiki. Ngati mwaona oposa kamodzi, chonde ikani manambala molingana ndi kukonda kwanu.

- |                               |                              |
|-------------------------------|------------------------------|
| — Kulemba makalata            | — Kusanthula Baibulo pa gulu |
| — Kupereka mayendedwe         | — Chipembedzo                |
| — Kuwayendera opalamula akale | — Kuyendera ma banja         |
| — Kulembera akayidi           | — Kukumanandi akayidi        |

Kodi inu munamangidwapo? Ngati “eya,” lembani tsiku, malo, chifukwa, kumasulidwa

Kodi munakhalako kosungira anthu amisala? \_\_\_\_\_ Ngati “eya,” liti ndi nthawi yotalika bwanji?

Kodi pali matenda omwe mumadwala? \_\_\_\_\_ Ngati “eya,” chonde fotokodzani:

Kodi mnagwirapo ntchito ndi akayidi? \_\_\_\_\_ Ngati “eya,” chonde forokodzani:

## Kodi mumalankhula zilankhulo zanji?

Kodi mumatha kuyimba? Ngati “eya,” zida zanji?  
Zungulidzani gulu la anthu omwe mukufuna kugwira nawo ntchito

## Amuna Akazi

Sainani apa \_\_\_\_\_ Tsiku

*Zindikirani: Ngati akazi akuloledwa kukatumikira ku ndende za abambo, onetsetsani kuti makhalidwe ndi mavalidwe abwino akutsatidwa. Chomwechonso ndi choona kwa azibambo omwe akutumikira ku ndende za akazi. Ngati kuli kotheka, mukhale ndi magulo a azibambo ndi azimayi. Maguluwa samangothandidza zovuta zikachitika komanso amathandi kupereka ubale wabwino pakati a azibambo ndi azikazi awo.*

Mukamaliza kulemba ogwira ntchito, aphunzitseni:

- Perekani pempho lanu la utumiki kwa iwo.
- Kambiranani malo omwe angagwire ntchito bwino.
- Gwiritani ntchito bukuli powaphunzitsa za utumiki wa kundende.
- Konzani ulendo wopita ku ndende komw muzikachitako utumiki kuti mukakunze chidwi chawo ndi kuchotsa omwe sakumva bwino ndi kumaloko.
- Onetsetsani kuti mwapedza chiroledzo cholowera ku ndende.
- Onetsetsani kuti ogwira ntchito anu aphunzira maphunziro onse aamene angaperekedwe ndi abusa kapena akulu akulu aku ndende.

#### **SITEPE YA CHISANU NDI CHIWIRI: Konzani msonkhano wanu woyamba**

- Onetsetsani kuti ogwira ntchito anu aphunzitsidwa bwino.
- Onetsetsani kuti aliyense wavala movemerzedzeka kapena modzilemekedza.
- Onetsetsani kuti wina ali yense ali ndi chidzindikiro cholowera mu ndende.
- Pali njira zosiyana siyana za momwe utumiki wa kundende ungachitikire. Ngati mwazindikira njira yopindura, osachedwa koma kumayigwiritsa ntchito kwambiri--koma osakhala ndi mantha kuyetsa njira zina. Onani Chaputala 6 pa malangizo omwe mungatsate pochita utumiki wa kundende.
- Onetsetsani kuti wina aliyetse akumvetsetse udindo wake mu utumiki. Chomwe angachite, nthawi zanji, ndi nthawi zopinga zomwe sakuyenera kutengapo gawo.

“Pitiridzani kufikira anthu ku ndende. Pali anthu ambiri muno ngati ine omwe amamkonda Ambuye--kapena omwe angakhale nagti ine—anthu amene mutha kusintha moyo waho ngati inu mungawafikire. Ngati Mpingo ungawaone ndikuwalandira ngati mbali ya Thupi la Khristu--aphunzitseni ndi kuwasamala mwa Ambuye ndi kuwaphunzitsa kuti aphunzite iwo omwe awazungulira—chitsitsimutso chikula mkazi muto mwa makoma”

-Mkayidi waku Texas  
-Karla Faye Tucker  
-Februale 3, 1998

### **MAFUNSO OZIYESA NOKHA A CHAPUTALA 3**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Lembani mwachidule masitepe oyambitsira utumiki wa kundende.

---

---

3. Kodi ndi mautumiki osiyana siyana ati omwe mungapereke ku ndende?

---

---

4. Kodi ndi njira ziti zomwe mungalembere ogwira ntchito mongodzipereka?

---

---

5. Kodi ndi njira ziti zomwe zaperekedwa mu chapatalacho zophunzitsira ogwira ntchito?

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 4**

## **Kulingana Ndi Akayidi**

### **VESI YOTSOGOLERA:**

**Izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu. (1 Yohane 5:13)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kufotokodza mene mungayambire kulingana ndi akayidi.
- Kelemba mwachidule malangizo olinganiza ndi akayidi.

### **CHIYAMBI**

Chaputala ichi ndi cha iwo omwe akufuna kutngapo gawo mu utumiki olunganiza ndi akayidi amu ndende. Chikufotokoza mmene mungayambire ndi kupereka malangidzo a kulinganiza kwa chitedzo ndi kopidula.

### **MMENE MUNGAYAMBIRE**

**Poyamba**, lumikidzanani ndi akulu akulu aku ndende. Ndende zina zimaperekamapologalamu omwe amalumikidza akayidi ndi “abwenzi omwe ali kunja.” Ngati ndendeyo kulibe mapologalamu amenewo, lankhulanani ndi abusaaku ndende pa mayina a omwe akufuna wina kuti awalembere kalata.

**Chachiwiri**, pedzani malamulo a momwe anthu amalumikidzirana ndi akayidi ku ndende imeneyo. Ndende zambiri ziri ndi malamulo omwe amayendetsa chilinganizo. Izi zimatsiyana pa ndende zosiyana. Ndende zina zimavomera kuti mutumikze ma sitampu ndi mapepara ena kudzera mu makalata, mabuku, ma thilakiti a Uthenga Wabwino, ma Baibulo, ndi makaseti a nyimbo. Pomwe ndende zina ziri njira zina zotumidzira izi, mwachitsanzo buku libwere ndi muthu yemwe walilemba. Ndende zina sidzilora kuti akayidi alandire zinthu izi kudzera mu makalata.

### **MALANGIZO PA CHILINGANIZO**

Awa ndi malangizo ena a momwe mungalinganizire mpindula ndi akayidi:

1. Mudzindikire pamene mukuwalembra akayidi kuti ambiri ayiwo amamva kukayikira, kuipidwa, ndi kusungulumwa.

-amakhala okayikira, chifukwa amakhala kuti achitiridwa nkhanza mumaubwenzi akale. Atha kumakayikira za malingaliro ano pomwe mukulemba: “Kodi mukupidula chani pochita idzi?” Muyetsetse kuti mukudze chikhulupiriro chawo, kulemekeza ndi kumvetsetsa kwawo.

-Akayidi amakhala oyipidwa chifukwa chokanidwa ndi anthu, pomwe inuno ndi m'modzi mwa anthuwo. Muwapatse akayidi chikondi chopada malire ndi kumvetsetsa.

-Akayidi amakhala osungulumwa chifukwa amakhala osiyanitsidwa ndi anthu, abwenzi, ndi mabanja awo. Ena kanidwa ndi mabanja awo. Mulungu wa thunthu popanda kulandira kalata utha kukhala ngati chaka, ndiye mudziremba mowirikidza ndi kuyankha mwachangu.

2. Pempherani kuti Mulungu akuthandidzeni kumvetsetsa kalati ina iriyonse ndi kukutsogolerani ku kayankhidwe kabwino. (Onani Chaputala 12 cha "Kulumikizana ndi Akayidi")
3. Ngati kuli kotheka, sizabwino kugwiritsa ntchito adiresi yakuyumba kwanu npoyankha makalata. Gwiritsani ntchito adiresi ya mpingo kapena utumiki wanu. Izi zizapewa zovvuta zokunza mtsogolo, mwa chitanzo, mkayidi wina kupeza adiresi ya kunyumba kwanu, mkayidi amene watulusidwa kundende pa belo kubwera kunyumba kwanu inu mutsakudziwa, ndi zina zambiri.
4. Mukambe momvetseteka kuyambira pachiyambi kuti inu simukuyanga'ana maubwenzi achikondi. Ndichapafupi akayida kukopeka mtima nanu ingakhale atakuonani koyamba, chifukwa cha kusungulumwa kwawo. Chifundo chanu athu otsachimvetsetsa bwinobwino. Ngati idzi zachitika, muchilankhule mu kalata wanu kapena kukumana kwanu. Mukhale ochenjera ndi aluso, koma olimba ku mbali iyi. Mautumiki ena amaometsetsa kuti amuna akulemberana ndi amuna anzawo chimodzimodzi ndi akazi.
5. Mutsagawi kenakalikonse kai nu komwe katha kugwiiritsidwa ntchito polimbana nanu.
6. Musatumidze ndalamu pokhapokha mutapemphera za ichi, ndipo mukudziwa kuti Mulungu akufuna kuti inu mutero. Ngati mwatumidza ndalamu, musabwereketse. Mutumidze ngati mphatso, koma musakhale oyembekedzera mphatso mtsogolo. Muonetsetse kuti ndalamu zatumidzidwa kudzera mu njira zoyerera za ku ndende.
7. Musalonjeze chithandizo cha kulemba ntchito, malo okhala, ndi zina zambiri, akatulutsidwa kundende pokhapokha utumiki omwe mukutumikira uli ndi kuthekera kochitsa idzi. Cholina chanu cholemba ma kalata ndikufuna kuperekwa chilimbikitso mwa Ambuye. Pempho lina lililonse likuyenera kuperekedwa ka akulu akulu oyenera.
8. Musakhale olalikira kwambiri mumakalata anu. Koyamba mukonze ubale wanu, kenako zizakhala zosavuta kugawana zinthu za uzimu. gawanani zinthu zomwe zimakuchitikirani zomwe zingapangitse mkayidi kumva kuti ali mbali imodzi ya inu ndi banja lanu.
9. Mukalata yanu ikanimo chinachiri chonse chomwe ndicholoredwa kutumidzidwa ngati:
  - zithunzi.
  - Nkhani zotsangalatsa.

- Mphatso ya sitampu kapena mapepala, mwa nthawi ndi nthawi, ngati andende amavomereza kutelo.
- Makatuni otsangalatsa.
- Ziphunzitso za Baibulo

“Ndi chinthu chachikulu--makalata omwe ndalandira---palibe mawu omwe ndingafotokodze ichi. Ndadalitsika kwambiri. Dzikomo, kuchokera pansi pa mtima wanga. Palibe mawu omwe angafotokoze zomwe izi zikutanthazuza kwa ine. Mtima wanga ukulira kuti ena nawonso athe kufotokoza chomwechi.”

-Mkayidi waku Texas  
-Karla Faye Tucker  
-Februale 3, 1998

MAYESO OZIYESA NOKHA A CHAPUTALA 4

- ### 1. Lembani vesi yotsogolera.

2. Kodi zinthu zofunikira zomwe mukuyenera kuchita ndi ziti pamene mukufuna kuyamba kulinganiza ndi akayidi?

3. Lembani mwachidule malangizo olinganiza ndi akayidi.

---

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 5**

## **Kuyendera Akayidi**

**VESI YOTSOGOLERA:**

**Kumbukilani am'nsinga, monga am'nsinga anzao; ocitidwa zoipa, monga ngati  
inunso adatero nanu m'thupi. (Ahebri 13:3)**

**ZOLINGA:**

- Kufotokoza chifukwa chimene kuyendera akaidi uli utumiki wofunikira.
- Kufotokoza mmene mungatengere gawo mu kuyendera kwa modzi modzi ndi akayidi.
- Kulemba mwachidule malangizo akuyendera kwapanokha ndi akayidi.

### **CHIYAMBI**

Akayidi ambiri ku ndende alibe yemwe amawayendere:

- Mabanja awo amakhala kutali ndi ku ndende kapena alibe mayendedwe owayeneredza.
- Mabanja awo anawakana kapena alibe banja.
- Abwenzia awo atha kuti anawaka.

Kuyendera akayidi ndi njira yomwe imaberaka zipatso ya utumiki waku ndende. Chaputala ichi chiukfotokoza ubwino wake, mmene mungengere gawo, ndi kupereka malangidzo a kukumana ndi akayidi.

### **KUFUNIKA KOKUMANA NDI AKAYIDI**

Kukumana ndi akayidi kwa modzi modzi ndi utumiki wabwino padzifukwa zotsatirazi:

-Moyo wina uliwonse ndi wa mtengo wake kwa Mulungu: “wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa” (2 Petro 3:9). Yesu anatumikira ku ma gulu a anthu, koma amakhala ndi anthu yotumikira mwa munthu modzi modzi (machitsanzo onani Yohane 4).

-Akayidi ambiri sangakumane nawo m’kumanano ya chipembedzo. Mwina anakhumuditsidwa ndi mikumano ya mbuyomo. Atha kukhala kuti akuopa kupita ku mikumano chifuka anenedwa kuti ndiofooka ndi akayidi ena ndi kuwapanga kukhala osatetezeka.

-Akayidi ambiri sanakumane ndi ubale woona, wa Umulungu, ndi wosaona nkhopo. Chomwe akudziwa ndi kuchitiridwa nkhanza ndi maubale osakhala bwino.

-Mwa ambiri aife--ndikosavuta kumasuka pokamba ndi munthu kusiyana ndi ku gulu. Mutha kukamba zambiri pa mikumano ya modzi modzi kusiyana ndi mmene mungachitire ku gulu. Akayidi atha kugawana nanu zokumana nazo, mutha kupemphera ndi kuwerenga limodzi Mawu a Mulungu, ndi kuyika kubale wa uzimu waphamvu.

-Inu mumakhala chowalumikidzitsa kubwerera kwa athu. Azakhala ndi m'bale owadikirira akadzatulutsidwa.

-Munthu modzi sangakhale ndi abale ambiri. Inu simungokhala m'dalitso, koma mudalitsika ndi ubale wanu ndi mkayidi.

### **KODI INU MUNGATENGEPO GAWO BWANJI**

Awa ndi malangizo omwe mungatsate pamene mukufuna kutengapo gawo pa mikumano ya modzi modzi ndi akayidi.

-Funsani za pologalamu yowonera akayidi ku ndende yomwe mukufuna kutengapo gawo. Ndende zambiri zili ndi mapologalamu okhadzikika olumukizanitsa ogwira ntchito yongodzipereka ndi akayidi.

-Ngati alibe pologalamu yokhadzikika, afunsemi abusa akundende kuti akulumikidzitseni ndi mkayidi. Ngati palibe m'busa, kumanani ndi wamkulu woyang'anira ndendeyo.

-Anthu amene akutumikira mcati mwa ndende ku gulu athaso kukhala gwero la bwino. Amadziwa akayidi omwe alibe munthu okumana nawo, kapena amaene angapindule ndi mikumanayo.

-ngati kuli kotheka sinthanani makalata ndi mkayidiyo musanayambe kukumana. Mukhala kuti mwapanga kale ubale mukamazakumana koyyamba.

### **MALAMULO A MIKUMANO**

Awa ndi malamulo okumanirana ndi akayidi:

-Mudzere mu njira zonse zoyerera kuti muvomeredzedwe ndi andende. Mutha kukhala kuti mukuyenera kulemba mu ma fomu, ku vomerezeka musanayambe kukumana ndi akayidi, kunyamula chidzindikiro choyenera, ndi dzina zambiri.

-Phunzirani ndipo mverana malamulo onse a kundende komwe mukufuna muzipitako. Malamulo atha kuphatikidza zinthu ngati, matsiku ndi maola omwe mukuyenera kukakumana ndi akayidi, mavalidwe oyenera, zachitedzo.

-Ndikwabwino kuti ngati mulu mwamuna mudzikumana ndi mkayidi yemwe alinso mwamuna. Idzi zimapewa maenje amaubwenzi osavomerezeka.

-Ndikwabwino kuti musapereke ndalamu kwa mkayidi kapena kwa apabanja pake. Ngati mukukhulupirira kuti ndikwabwino kutero ndiponso Mulungu akukutsimikidzirani kuti mutero, ndikwabwino kupereka chithandidzo chanu kudzera kwa abusa aku ndende kapena anthu ena akundendeko.

-Ngati mwapanga ubale wabwino ndi mkayidi, kumakhala kosavuta kugawana Uthenga Wabwino ndi iwo.

-Osalalikira kapena kuphunzitsa. Mufunzeni Mulungu momwe mungagawire chikondi chake ndi Mawu ake munjira yoti alandiridwe. Mkayidi akakhala okhulupirira, pitirizani kumuphunzitsa Mawu a Mulungu.

-Ngati kuli kololedwa, perekani Baibulo kwa mzanuyo ndi mabuku ena aza Mulungu. Dalirani pa malamulo akundende, mutha kuvomeredzedwa kutumidza idzi kudzera pa kalata, mupitinse nokha, kapena apatsireni abusa kuti akapereke.

-Pokhapokha muthakhala kuti mwaphunzitsidwa kapena ndinu muli ndi mphatso ya ulangidzi, musatenge gawo iri mu ubwenzi wanu. Inu muli kumeneko ngati abwenzi. Inu musanve ngati kuti mukuyenera kuperekwa yankho ku funso linalirironse lomwe labwera.

-Ngati paubwenzi, khalani osunga chinsisi. Sungani uthenga womwe mwagawana ndi bwenzi lanu mwachinsi.

-Nthawi zonse zindikirani kuti inu muli kumeneko ngati oyimirira Ambuye Yesu Khristu-- osamangotha ndawi yanu yonse kukambirana nkhani za uzimu. Chedzani ngati mmene mumachenjera ndi mzanu wakunymba kwanu. Kambiranani zinthu zomwe zikuchitika, tsekani limodzi, mafukiranani ndi bwenzi lanu!

## **MAYESO OZIYESA NOKHA A CHAPUTALA 5**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

2. Kodi kuyendera akaidi ndi utumiki wofunikira motani?

---

---

3. Lembani mmene mungatengere gawo mu kuyendera kwa modzi modzi ndi akayidi.

---

---

4. Lemnani mwachidule malangizo akuyendera kwapanokha ndi akayidi.

---

---

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 6**

## **Kuchita Mikumano Ya Gulu**

### **VESI YOTSOGOLERA:**

**Koma Iye, poona makamuwo, anagwidwa m'mtima ndi cisoni cifukwa ca iwo, popeza anali okambululudwa ndi omwazikana, akunga nkhosa zopanda mbusa.**  
**(Mateyu 9:36)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kudzindikira mitundu yosiyana siyana ya mikumano ya gulu yomwe ingachitike ku ndende.
- Kulemba mwachidule malangizo a kapangidwe ka mikumano ya gulu.

### **CHIYAMBI**

Ndende zambiri zimapereka mwayi ya utumiki wag ulu kwa akayidi. Chaputala ichi chikukamba za mitundu yosiyana siyana ya mautumiki a gulu ndi malangizo a kapangidwe ka mikumano ya gulu.

### **MITUNDU YA MIKUMANO YA GULU**

Pali mitundu yambiri ya mikumano ya ma gulu a chi Khristu yomwe ingachitike kundende:

- Mikumano ya kulambira
- Kusanthula Baibulo
- Makalasi azamayimbidwe (Kuphunzitsa oyimba, kapana kapena kwaya ya chipembedzo chakulambira cha kundende)
- Mikumano ya mayimbidwe ndi zitsunzo.
- Zolemba zachi Khristu
- Magulupo ang'ono ang'ono opereaka chithandidzo cha chikristu kwa akayidi omwe ali ndi mavuto a chilakolako ndi nkhawa.
- Maphunziro a Baibulo
- Makalasi a ophunzira a okhulupirira atsopano

Kumbukirani kutsatira malangizoomwe aperekedwa mu Chaputala 3 cha bukuli.

### **KUCHITITSA MIKUMANO YA GULU**

Awa ndi malangizo omwe mungatsate pamene mukuchititsa mikumano ya gulu ku ndende.

## **NTHAWI:**

Ndende zambiri zimayendetsera mu ndandanda wokhwima. Mikumano yonse iziyamba ndi kutsiriza mu nthawi yake.

## **NYIMBO:**

Nyimbo pa nthawi ya chipembedzo zikuyenera kulimbikitsidwa. Nyimbo zomwe zitha osamvetseteka ndi anthu okhala ku ndende zikuyenera kuti zisamayimbiwe. Ngakhalenso nyimbo za nkhawa ngati “Palibe Yemwe Akuziwa Mavuto Omwe Ndawaona.” Ngati mukugwiritsa ntchito nyimbo za m’buku, muyetsetse kuti muli ndi mabuku okwanira. Nthawi zonse pephani chiroledzo kkuchokera kwa m’busa wa ku ndende musanakonze mkumano wina uliwonse wa mayimbiwe.

## **PEMPHERO:**

Awa ndi maganizo a nthawi yapemphero

-Nthawi zonse pemphero lizikhala lalifupi ndilokamba zinthu zofunikira kupatula Mzimu Woyeraya akayenda mu njira yapaderadera. Pemphero lalitali siringangopangitsa mapemphero kuhala osasangalatsa komando litha kupangisa kuti asakumvetseteni ndi kumati, “Anthu awa akusowa mapemphero aatali.”

-Nthawi zambiri muzipempherera anthu omwe ali odwala, osongonekera ubongo ndi nkhondo ya uzimu ya akayidi, zokhumba zawo komanso za mabanja awo. Muzipemphereraro ogrira ntchito ku ndende.

-Ndizosalakwika osatseka mmaso (kapena membala modzi wag ulu lanu osaseka mmaso) ndicholinga chokhazikisa bata.

## **KEWERENGA MALEMBO:**

Munthu amane akuwerenga malembo pa nthawi ya chipembedzo, “akunena” mawu a Mulungu. Mawu awerengedwe momveka bwino, mopereka ulemu ndi mwamphamve (onani Nehemiya 8:8). Munene momveka bwino, musanayambe kuwerenga, pomwe Malemba akuchokera (buku, chaputala ndi mavesi). Apatseni nthawi omwe ali ndi ma Baibulo kuti apedze ndime yomwe mukufuna kuwerenga. Mawu anu azifikira anthu mwe ali kumbuyo kwenikweni. Muyime njo ndikulankhula momveka bwino. Muwerenge Mawu a Mulungu mwaluso mopereka chikoka ku mitima ya akayidi.

## **MAUMBONI**

Ngati mwapemphedwa kuti muperekere umboni, musatenge ngati ichi ndi mwayi wanu woti mulalikire. Musagwiritsa mawu ovuta kumvetsa ngati, “Pomwe ndinabwera mu uthenga” kapena “Nditalandira choonani.” Ndibwino kugwiritsa ntchito mawu ngati awa “Pomwe ndinakhala m’Khristu” kapena “Nditalandira Yesu khristu ngati Mpulumutsi wanga.”

Umboni wanu uzikamba za Khristu:

- A. Nthawi zonse muzikamba zomwe Khristu wachita kai nu ndi/kapena ndi banja lanu, kukamba zinthu zomwe zingatukule chikhulupiro cha akayidi.
- B. Muonetsetse kuti ukhale waufupi, m'phindi 2-3. Musaukambe onse. Zindikirani kuti mukugwira ntchito mu nthawi yochepa. Mukalankhula kwambiri, mupangisa kuti olalikira akhale ndi nthawi yochepa.
- C. Nthawi zonse muzilankhu momveka bwino, makamaka pakakhala kuti chimkuza mawu palibe, ndiye mukuyenera kumvedwa ndi wina aliyense.

### **KULALIKIRA KAPENA KUPHUNZITSA**

Uthenga womwe wakonzedwa kulalikidwa kapena kuphunzitsidwa ku ndende usapyole mphindi 30 (pokhapokha ngati Mzimu Woyeru akuyenda). Akayidi ambiri satha kumvetsera kwa nthawi yayitali. Komanso inu mukufunika kuthesa uthenga nthawi yabwino kuti mumalizinse china chirichonse ndi kuyendera akayidi modzi modzi (mkumano ndi wabwino kwa iwo).

Uthenga wanu ukhale ogwirizana ndi akayidi. Ukhale ndi zimene mukuziwa za anthu omwe mukuwalalikira. Uthenga wokuza chikhaldwe ndi olumbikitsa ndi wabwino. Ngati mukulankhula zamachitidwe oyipa, nthawi zonse gwiritsani “ife” kuonetsera kuti imu muli nawo limodzi.

Zinthu zosatirazi **zisachitike** mu utthenga wanu:

- Mutsadzudzule akayidi. Adzudzulidwa kale ndi abwenzi, abale, owayimirira pa mulandu ndi oweruza milandu.
- Osalankhula zinthu zomwe zitha kutanthauzoridwa udyo ndi ogwira ntchito ngati kuphwanya chitedzo.
- Osaonera pansi zipembedzo zina.
- Osaoonetsera nkhalibe woziyeretsa kwambiri.
- Osamafunsa mafunso ovuta, kapena kuganiza kuti gulu likutsutsana namu.
  
- Ngati liri gulu laling’ono, khalani mozungulira.
- Pa gulu laling’ono limbikitsani kuti aliyense atenepo gawo. Njira yofunsa mafunso ndi kuyankha ndiyabwino. Musalole kuti munthu modzi aziyankhula yekha.
- Onetsetsani kuti wina aliyense ali ndi Baibulo ndipo alimbikitseni kuti muziwerenga limodzi.

### **KULOWA NDI KUTULUKA MU MALO ACHIPEMBEDZO**

Ndibwino, makamaka pa gulu lalikulu, kukhala ndi dongosolo lokhazikika yolowera ndi kutuluka mu malo omwe mukuchitiramo chipembedzo. Ndende zina zimawauba akayidi kuti aziyimba nyimbo kuti onse akhale muchimodzi. Afunseni akayidi ena kuti atsalire chipembedzo chikatha kuti abwenzerense chinachiri chonse chimake.

## **MAFUNSO OZIYESA NOKHA A CHAPUTALA 6**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Lembani mitundu yosiyana siyana ya mikumano ya gulu yomwe ingachitike ku ndende.

---

3. Lemabani mwachidule malangizo a omwe aperekedwa muchapatalachi mu ma dera otsatirawa:

Nthawi\_\_\_\_\_

Nyimbo\_\_\_\_\_

Pemphero\_\_\_\_\_

Kuwerenga  
malembo\_\_\_\_\_

Umboni\_\_\_\_\_

Kulowa ndi Kutuluka malo a  
mapemphero\_\_\_\_\_

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 7**

## **Kutumikira ku Mabanja a Akayidi**

### **VESI YOTSOGOLERA:**

**“... ndipo mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a dziko lapansi.” (Genesis 12:3)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kufotokoza chifukwa chimene mabanja a akayidi nthawi zonse amakhala pamavuto.
- Kudzindikira njira zaome mungatumikire mabanja a akayidi.
- Kulemba mwachidule malangizo a kutumikira ku mabanja a akayidi.

### **CHIYAMBI**

Mabanja ambiri akukhudzidwa chaka ndi chaka pokhala ndi modzi wokondedwa amene amalowa ku ndende. Mabanja ambiri amasweka ndi kudzadzidwa ndi kusungulumwa, nkhawa ndi kumva klinikwa. Mabanja ochepta ndi amene amalandira chithandidzo chokwanira kuchokera ku mpingo.

Mulungu anamuudza Abrahamu kuti kudzera mwa iye, “ndipo mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a dziko lapansi.” Ngati olowa auzimu a Abrahamu, ifenso titha kudalitsa mabanja. Chaputala ichi chikukamba njira zomwe inu ndi/kapena mpingo wanu mutha kutengapo gawo potumikira mabanja a akayidi.

### **KUMVETSETSA MAVUTO**

Pamene membala wa pa banja wamangidwa, nthawi zambiri izi zimalenga nkhawa, mantha, ndi kusakhadzikika kwa apabanja awo, ana kapena makolo. Kumangidwa kumabweresa mavuto a akulu pa banja. Vuto loyamba ndi lakuti mmodzi wa pa banja wamangidwa chifukwa chophwanya lamulo. Vuto lachiwiri ndilakuti banja limagawikana. Kutaya munthu chifukwa choti wamangidwa ndi chimodzimodzi kuti wamwalira.

Ana amakhala ndi manyazi ndi kutayika pamene makolo awo amangidwa. Atha kusinthidwa kokhala, kuyamba kukhala ndi achibale, Anansi, kapena kukakhala malo osungirako ana amasiye ndi osowa. Ena satha kukhala ndi mwayi okaona makolo omwe amangidwa chifukwa cha lamulo lochokera ku khoti, mtunda wochokera ku ndende, kapena chuma cha anthu omwe akuwasunga sangakwanitse kuti athe kumakana makolo awo (mtengo wa mayendedwe, chakudya, malo ogonamo).

### **MENE MUNGATHANDIDZIRE MABANJA A AKAYIDI**

Zotsatirazi ndi njira zomwe mungagwiritse ntchito potumikira mabanja a akayidi:

**Mayendedwe ndi kuchereza:** Perekani mayendedwe kuti banja lithe kukamuona wokondedwa wawo. Ngati mumakhala kufipi ndi ndende, perekani malo oti apabanja athe kugona pamene akukamuona wokondedwa wako. Kafukufuka amasonetsa kuti mabanja omwe amakhala limodzi ndi kumakamuona okondedwa wawo kundende ali ndi kuthekera kwakukulu kopangitsa kuti wokondedwa wawo asamakhale moyo wosungulumwa ndi kukanidwa.

**Uthenga:** Banja silingathe kudziwa momwe angapedzere uthenga--zinthu ngati matsiku okalowera ku bwalo la milandu, momwe angapitireko, kapena mene angapedzere munthu wodziwa malamulo. Inu mutha kukhala othandidza ngati mukudziwa mene zamalamulo zimayendera.

**Mwayi wa ntchito:** Ngati wasala pang'ono kumasulidwa, mkayidi atha kuzafuna mwayi wantchito.

**Malo okhala, chakudwa, zovala, ndi chuma:** Banja litha kufuna malo okhalapo, chakudya, kapena chuma kuti athandizike. Ngati inu kapena mpngo wanu umapereka chithandidzo cha chuma, mabuku a ku malo osaungira ndalamu azigwiritsidwa ntchito pofuna kupereka chithandidzo cha anthu, komanso ngati mwawapedzera malo okhala mudzionetsetsa kuti ndalamu mukupereka nokha kwa eni malowo.

**Kupereka uphngu:** Banja lonse kapena membala wa banja atha kufuna uphungu kuti the kuthana ndi mavuto.

**Kuperaka mphatso:** Nthawi ya khirisimasi ndi masiku akubadwa ndi ovuta pa ana ndi makolo awo amene amangidwa. Njira imodzi yomwe mungathandidzire ndikugula mphatso za khirisimasi ndi masiku akubadwa, akuteni, kaperekeni kwa anaomwe makolo awo amangidwa. Idzi dzimakondweretsa akayidi ndi ana awo.

**Nyumba yamapemphero:** Chinthu chofunikira kwambiri chomwe mungapereke kwa mabanja a akayidi ndi kupereka kwa iwo mpingo wokonda, wothandidza, ndi wowalandira.

### **MMENE MUNGALUMIKIDZIRANE NDI BANJA LA MKAYIDI**

Pali zinthu ziwiri zofunikira zomwe mukuyenera kuchita musanayambe kulumikidzanandi mabanja a akayidi.

-Fufuzani kwa abusa aku ndende or akulu akulu aku ndende kumene mukutumikira. Onani ngati kuli malamulo omwe amaletsa izi kapena dongosolo lokhadzikika yomwe inu mungatsatire.

-Katengeni chiloledzo cholembedwa kwa mkayidi kuti banja lake ndi andende adziwe kuti muli ndi chivomeredzo chake. Chiroledzo chimaonetsera cholinga chanu cholumukidzirana ndi banja lake. Inu mutha kugwiritsa ntchito kapena kusintha fomu iri mutsiyi

### **Fomu Yopempha Chirolendo Chokumana ndi Banja**

Ndife okondwa kutsatira pempho lanu lofuna kuti ife tilumikizane ndi apabanja lanu kuti tika pereke chirimbikitso, uphungu, maphunziro a Baibulo, ndi zosowa zina zikafunikira kutero—koma tikufuna chivomeredzo chanu. Chonde malidzitsani fomuyi. Chonde sindikidzani:

Dzina\_\_\_\_\_

Numbala ya chidzindikiro ya mkayidi\_\_\_\_\_ Malo oganamo\_\_\_\_\_

Ndende\_\_\_\_\_ Malo omwe iri \_\_\_\_\_

Chonde Lumikidzanani ndi:

|                                      |                |              |                           |   |
|--------------------------------------|----------------|--------------|---------------------------|---|
| <b>Dzina la Membala<br/>wa Banja</b> | <b>Adiresi</b> | <b>Lamya</b> | <b>Ndi ndani<br/>Wanu</b> | <b>Chifukwa chimene<br/>Mukufunira kuti<br/>ife Tilumikidzane<br/>ndi iwo</b> |
| _____                                | _____          | _____        | _____                     | _____   |
| _____                                | _____          | _____        | _____                     | _____   |

Saini yanu\_\_\_\_\_ Tsiku\_\_\_\_\_

Kuvomweredzedwa ndi m'busa kapena mkulu wa ndende:

|            |       |              |
|------------|-------|--------------|
| <b>Ndi</b> | _____ | <b>Tsiku</b> |
| Saini      | _____ | _____        |

Kutimba lamya ndi kukumana kosatenga nthawi kuyambitse utumikiwu. Pokwaniritsidwa kwa mkumano, kapena lamya, pempherani pemphero lalifupi. Pokakumana kachiwiri, mutenge buku lomwe mkayidi akugwiritsa ntchito kuti adzikulira limodzi mu uzimu. Ngati sakutsangalatsidwa nalo, pitilidzani kukumana nawo mwaubale ndi kulimbikitsa. Nthawi zonse yetsetsani kulunjikitsa macheza anu kuzinthu zomwe akukumana nazo komanso ndi mapulani amtsogolo a banja ndi ntchito. Thetsani machedza omwe akubweretsa maganizo osakhala bwino. Mukamakumana, banja litha kugawa mavuto amene akukumana nawo. Ngati pakufunika thandidzo, funsani ngati kuli koyenera kuwathandidza.

*Zindikirani: Ndikwambino kuti banja lonse lidziyendera pamodzi. Amuna atsayendere mkazi wa mkayidi ali yekha, kapena mkazi kuyendera mwamuna wa mkayidi yekha.*

Pamene mukugwira ntchito ndi banja la mkayidi, tsungani zinthu zonse mwachinsisi. Gawani zinthu zomwe mwavomeredzedwa kutero. Inu mutsatengepo gawo mu dzinthu zamalamulo kapena kukamba mavuto omwe ali pakati pa mkayidi ndi banja lake.

## **MAYESO OZIYESA NOKHA A CHAPUTALA 7**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Ndihifukwa chani mabanja a akayidi nthawi zambiri amakhala pamavuto?

---

3. Kodi ndi njira ziti zomwe mungatumikire mabanja a akayidi?

---

4. Kodi ndi zinthu ziti ziwiri zomwe mukuyenera kuchita musanayambe kukumana ndi banja la mkayidi?

---

5. Lembani mwachidule malangizo a kutumikira ku mabanja a akayidi.

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

## **CHAPUTALA 8**

# **Kutumikira Ku Akayidi Omwe ali Pachigamulo Chokanyongedwa**

### **VESI YOTSOGOLERA:**

**Kubuula kwa wandende kufike kuli Inu; Monga mwa mphamvu yanu yaikuru  
lolani ana a imfa atsale. (Masalmo 79:11)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kufotokoza mmene mungayambire utumiki wa akayidi omwe ali pachigamulo chokanyongedwa.
- Kufofokoza malangizo autumiki wa akayidi omwe akukanyongedwa
- Kufotokoza mmene mungamukonzeretse mkayidi yemwe akukanyongedwa.

### **CHIYAMBI**

Ndende zina ziri ndi malo omwe amatsungiramo akayidi omwe agamulidwa kuti akanyongedwe. Akayidi awa nthawi zambiri amatsungidwa kumalo achitetedzo chochuluka. Chaputala ichi chakunzedwa kuti chikuthandidzeni kukatumikira ku akayidi omwe ali pa nzere okanyongedwa.

### **MMENE MUNGAYAMBIRE UTUMIKI WA AKAYIDI OMWE AKUKANYONGEDWA**

Utumiki wa akayidi okanyongedwa--ngati mautimiki ena onse aku ndende--ukuyenera kuvomweredzedwa ndi akulu akulu oyang'anira ndende. Nthawi zambiri simungapatsidwe mwayi pompo pompo kuti muyambe utumiki wa akayidi okanyongedwa. M'busa kapena wamkulu wakundende amfuna akuonene kaye momwe mukugwirira ntchito mu zigawo zina za ndene--mu utumiki wa modzi modzi kapena wagu.

Ndende zina sizilola utumiki wag ulu ku akayidi omwe ali pachigamulo chokanyongedwa Kamba ka chitedzo. Inu musagwe ulesi--munthu kuloledwa kutumikira kwa modzi modzi pakudzera pokumana kapena kulemba makalata. Izi zitha kukhala zabwino, pakulimbikitsa ubale ndi kugawa Uthenga Wabwino. Komanso zitha kukhala njira yam wayi wotumikira ku gula la akayidi mtsogolo.

### **KUTUMIKIRA KU AKAIYIDI OKANYONGEDWA**

Ngati mukutumikira pakulemba makalata kapena kukumana ndi akayidi okanyongedwa mwa modzi modzi, onaninso Chaputala 4 ndi 5 a bukulu pa malandizo akalembedwe ndi kakumanidwe. Ngati mukupanga utumiki wotumikira gulu, onani Chaptuala 6, 11, ndi 12. Malangizo omwe ali mumachaputala awa athanso kugwiritsidwa tchito ku akayidi omwe akukanyongedwa.

Malamulo apaderadera a utumiki wa akayidi okanyongedwa ndi awa:

-Nthawi zina pamakhala malamulo osiyana akakumanidwe, kalembedwe, kapangidwe ka misonkhano ya akayidi okanyongedwa chifukwa cha chitetedzo. Funsani za malamulowa ndipo muziwasata nthawi zonse.

-Ngati mkayidi okanyongedwa akuti sanalakwe, inu si mbali yanu kuti mukawayimirire. Pali nyengo zambiri zimene akayidi okanyogedwa amafulidwa zitatsimikidzidwa kuti iwo ndiwopanda mulandu. Ngati akuti nndiosalakwa, pempherani nawo kuti Mulungu alowererepo ndikuti chilungamo chioneke.

-Kumva kulekanitsidwa, ndi kukhala opanda chiyembekedzo ndi zapali ponse chifukwa akayidi okanyongedwa amalekanitsidwa, nthawi zambiri amakhala ali mu ma selo awo, komanso amapasidwa mwayi wochepa wotengapo gawo ku mapologalamu aku ndende. Mutha kuthandiza pakukhala bwenzi lowalimbikitsa ndikuwapansa njira zomwe azipanga pa nthawi yomwe akungokhala (magamu, zinthu zowerenga, zi zinthu zina zomwe ziri zoledzedwa).

-Anthu amagamulidwa kukanyongedwa chifukwa cha mulangu womwe anapalamula. Ena amatha kuvomereza kulakwa kwawo, koma osaonensa chisoni pa kulakwa kwawo. Mukuyenera kukhala ndikuthekera kowalandire mmene aliri ndipo--kudzera mu chikondi ndi mphamvu ya moyo wa Mulungu yosintha--atsogolereni ku malo omwe akuyenera kukhalako.

-Mukuyenera kukhala ndikumvetsetsa kwambino kwa kusintha kwa m'Baibulo: "... ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano" (2 Akorinto 5:17). Anthu atha kufunabe kuti mkayidiyu alipire zolakwa zake ndi moyo wake, Koma Mulungu wamukhululukira pomwe ali cholengedwa chatsopano. Iwo salinso munthu amnena anapalamula uja.

-Onetsetsani kuti mkayidi amvetsetse kuti kubadwanso mwatsopano sikutanthauza kuti Mulungu awapulumutsa ku chilango cha imfa. Gawanani Ahebri 11 ndi iwo. Anthu ambiri a Mulungu anapulumutsidwa ku imfa, koma enanso anafa. Ena anapulumutsidwa kutuluka ku ndende, ena sanapulumutsidwe. Mulungu akufuna kuwapasa chikhulupiriro pamene akufa komanso pamene akukhala ndi moyo.

-Pitilizani kuimabe mu chikhulupiriro ndi mkayidi amene akukanyongedwa mpakana mwayi wonse wopanga apilo wakanika—koma musakhale ndi mantha kuwathandidza ngati imfa yadziwikiratu.

Pali munthu yemwe akuyenera kumukhululukira? Athangatireni kutero.

-Kodi alipo omwe akuyenera kuwapepesa ndikupempha chikhululukiro chawo—ozunzidwa, mabanja awo, banja lake kapena abwenzi ake? Athangatireni kutero.

-Ngati ali ndi ana achichepere alimbikitseni kuti awalembere kalata yomwe ingadzapatsidwe kwa iwo akazakula.

-Kambiranani nawo za imfa yawo, ndipo chilungamo choti ali okhulupirira, palibe chinthu choti achite nacho mantha. Wina aliyense ali ndi nthawi yake yoyikika kuti adzafa. Kusiyana kwa iwo ndi okhulupirira ena ndikoti iwo akuziwa tsiku lomwe azafe. Ichi chitha kukhala chinthu chabwino, chifukwa chimawapansa nthawi yochita ndi kulankhulo zoyenera kuchitidwa ndi kulankhulidwa. Pakuti kwa okhulupirira, imfa inamedzedwa m'chigonjetso:

**Taonani, ndikuuzani cinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipoife tidzasandulika. Pakuti cobvunda ici ciyenera kubvala cisabvundi, ndi caimfa ici kubvala cosafa. Ndipo pamene cobvunda ici cikadzabvala cisabvundi ndi caimfa ici cikadzabvala cosafa, pamenepo padzacitika mau olembedwa, Imfayo yamezedwa m'cigonjetso. Imfawe, cigonjetso cako ciri kuti? Imfawe, mbola yako iri kuti? (1 Akorinto 15:51-55)**

Imfa imatimasula ku uchimo, mayetsero, ndi kuzophinja za moyo:

**Pakuti tidziwa kuti ngati nyumba ya pansi pano ya msasa wathu ipasuka, tiri naco cimango ca kwa Mulungu, ndiyo nyumba yosamangidwa ndi manja, yosatha, m'Mwamba. Pakutinso m'menemo tibuula, ndi kukhumbitsa kubvekedwa ndi cokhalamo cathu cocokera Kumwamba; ngatitu pobvekedwa sitidzapezedwa amarisece. Pakutinso ife okhala mu msasawu tibuula, pothodwa; si kunena kuti tifuna kubvulidwa, koma kubvekedwa, kuti caimfaco cimezedwe ndi moyo. (2 Akorinto 5:1-4)**

**Imfa ya okondedwa ace Nja mtengo wace pamaso pa Yehova.  
(Masalmo 116:15)**

Pa imfa, okhulupirira amalowa mu kupezeza kwa Mulungu:

**koma tilimbika mtima, ndipo tikondwera makamaka kusakhala m'thupi, ndi kukhala kwathu kwa Ambuye. (2 Akorinto 5:8)**

-Athanzidzeni kuti adziyang'ana pa moyo wamuyaya ndi zinthu zabwino zomwe zikuwadikirira kumwamba. Onani Chibvumbulutso 21 ndi 22.

Ngati mkayidi okanyongedwa wakupemphani kuti inu mudzakhalepo pa tsiku lawo lokaphedwa popereka chirimbikitso cha uzimu, chitani choncho ngati akundende akuvomerezani. Mutha kuthandidza kupangisa kukhala tsiku lawo lolandiridwa ku mwamba osati tsiku lachiopsyezo—chifukwa, mkayidi amene wakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu apita kuchokera ku imfa kunka ku kupezeza kwa Mulungu.

**Kulibe Zotsekulira Zitseko Kuno**  
**Yolembedwa Ndi Catherine Thompson**  
**Wogamulidwa Kukanyongedwa kundende Ya Azimayi yaku California**

“Ndapedzedwa ndi abwenzi kangapo kuti ndilembe maganidzo anga. Koma ndinadada ndi maganidzo amenewo. Koma matsiku angapo apitawo munthu wina akuyang’ana malo anga ogona anafunsa mene ndimakhalira pa ukayidi okanyongedwa ndikumayang’ana anthu omwe angatenge moyo wanga. Munthu wina anafunsa ngati ndiri bwino chifukwa sindimadandaua nthawi zonse ndinali wosangalala.

“palibe modzi yemwe amadzindikira kuti ndinamwetulira muchoonadi pa June 13, 1990. Tsiku lotsatira, bwenzi langa lapamtima, ndi wachikondi wa moyo wanga anatengedwa kuchoka kwa ine pakuohedwa. Imenelo inali tsiku lomalidza lomwe ndinaki ndi chimwemwe chenicheni.”

“Pali zinthu zomwe ndimangodzitenga pa moyo wanga zomwe pano ndimaziona ngati ndi zamwayi, ngati kuyimbiridwa lamy, kupita kunja kukapitidwa mphepo, kapena zinthu zophweka ngati kutsegula chitseko kapena zenera. Kulibe zotsekulira zitseko kuno. Chitseko changa chimatsegulidwa ndi mphamvu yamagetsi.”

“Ngai mzika ya mziko, ndinavota motsutsana ndi chilango chonyongedwa. Ndimamva kuti Mulungu anawerenga matsiku athu apadziko lapansi ndipo sapereka mphamvu kwa munthu kuti awasinthe. Palibe wina, kaya chigawenga kaya anthu, yemwe ali ndi mphamvu yokapha munthu. Ndimangodikirira kuti dziko lipedze yemwe angandiyirire pamulandu wanga chifukwa sindingakwanitse kugula chilungamo. Ku dziko, chilungamo, ngati china chirichonse, chimabwera ndi mtengo wawukulu.

“Pa nthawi ino, matsiku anga amatha ndikukweza ulemu wanga. Ufulu wanga unatengedwa, mtima wanga unasweka, kumwetulira kwanga kuwonongedwa, koma palibe munthu yemwe angatenge ulemu wanga.”

## **MAFUNSO OZIYESA NOKHA A CHAPTALA 8**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

---

2. Lemani mwachidule mlingaliro omwe aperekedwa mu chaputala ichi a mmene mungayambire utumiki wa akayidi omwe ali pachigamulo chokanyondegwa.

---

---

3. Fotokozani malangizo autumiki wa akayidi omwe akukanyongedwa

---

---

---

4. Fotokozani malingaliro omwe aperekedwa mu chaputala ichi a mmene mungamukonzeretse mkayidi yemwe akukanyongedwa.

---

---

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

## **CHAPUTALA 9**

### **Utumiki Wa Akayidi Omwe Amasulidwa**

#### **VESI YOTSOGOLERA:**

**...kuti utsegule maso akhungu, uturutse am'nsinga m'ndende, ndi iwo amene akhala mumdima, aturuke m'nyumba ya kaidi. (Yesaya 42:7)**

#### **ZOLINGA:**

- Kudzindikira zosowa za akayidi omwe atulusidwa ku ndende.
- Kufotokoza mitundu ya utumiki wa akayidi omwe atulusidwa kundende.
- Kulemba masitepe poyambisa utumiki wa akayidi omwe atulusidwa ku ndende
- Kudzindikira udindo wanu mu utumiki wa akayidi omwe atulusidwa ku ndende

#### **CHIYAMBI**

Akayidi ena amatulusidwa ku ndende akagwira ukayide nthawi imene anadzengedwa kuti agwire. Koma mu nyengo zina akayidi akamaliza mbali ya nthawi yimene akuyenera kugwira ukayidi, akayidi amatha kuloledwa kupita mapaso pa oweruza milandu. Akalolezedwa kupasidwa belo asanamalize kugwira nthawi onse ya ukayidi wawo, amamasulidwa koma amauzidwa kuti azikwanirtsa zinthu zina, monga kumakazionetsa ku ndende pafupi pafupi, osakhala limodzi ndi anthu omwe anali zigawenga, ndi kukanidzidwa kokhuda makhalidwe ndi kagwiridwe kantchito.

Akayidi omwe amasulidwa kuchokera amakhala ndi zosowa zambiri pamene akubweranso kudzakhala limodzi ndi anthu. Chaputala ichi chikuthandidzani kudzindikira zosowazi, kumvetsetsa mitundu yosiyana siyana ya utumiki wa akayidi omwe amasulidwa, ndi kutanthauza udindo wanu potumikira akayidi omwe atulusidwa ku ndende.

#### **ZOSOWA ZA AKAYIDI OMWE AMASULIDWA KUMENE**

Akayidi ena ndiwodalitsika kuti pomwe atuluka kundende amafikira ku ma banja kpena mipingo yomwe imawapasa chithandizo chonse chomwe akufuna, koma ngati alibe ubale umenewo utumiki wa kunya kwa ndende ndi wofunikira. Munthu aliyense ndiwosiyana ndi mzake ndipo ali ndi zosowa zosiyana ndi mzake, koma pali zosowa zina zomwe ziri zofanana zomwe zimapezeka pa akayidi onse omwe aamasulidwa kumene.

-Akuyenera kuti alandiridwe mu mpingo wakudera komwe amakhala omwe unamusamale ndi kumuthandidza kuti akule mu uzimu. Muyitaneni kuti mupite limodzi ku kachisi. Mukhale nawo limodzi komanso ayitaneni kuti mukadye nawo limodzi chipembedzo chikatha.

-Akusowa malo okhola, chakudya, ndi zovala.

-Akusowekera maphunziro a ntchito za manja ndi/kapena kupeza ntchito.

-Atha kusowekera uphungu wazachuma. **zindikirani:** Musapereke chithandidzo cha chuma nokha kwa munthu yemwe watulusidwa kundende koma ngati mukufuna kuthandidza mukuyenera kudzera kwa mpingo wanu.

-Uphungu wa banja ndiwofunika ngati akufuna kuti alumikidzanenso ndi banja lake.

-Atha kusowanso uphungu wapaderadera kuzilakolako za mankhwala ozungudza umbongo. Okhulupirira amene aperaka moyo wawo kwa Khritsu atha kukumana ndi mayesero azilakolako ngati nkhondo yawo yoyamba ya uzimu.

-Ngati anamangidwa kwa nthawi yayitali, atha kufuna chithandidzo ngakhale pa zinthu zowoneka zazing'ono chifukwa akayidi amakhala ndi mwayi wochepa wopanga chisankho.

-Akusowekera abale omwe ali olimba kuti adzimukonda ndi kumulandira, kupemphera naye ndi kumupempherera, ndi kumuthangatira kuti athane ndi zovuta zomwe zingadze.

Komanso, mukuyenera kuti mudziwe zambiri za mkayidiyo asanamasulidwe. Zomwe mungapeze zizakuthandizani mu utumiki wanu. Dzindikirani luso lake ndi maphunziro ake. Dziwani komwe akukhala (nthawi zina akayidi amafunikira kuti apite ku malo ena). Kambiranani ndi abusa ndi akulu akulu akundende oyenera za idzi musanakambirani ndi mkayidiyo. Musalonjeze kalikonse ngati mukudziwa kuti simugakwanise kumamuyendera.

### **UTUMIKI WA KUNJA KWA NDENDE**

Pali mautumiki osiyana siyana a kunja kwa ndende omwe mungayambise amene mkayidi atha kutumidzidwako:

**-Banja la lakati la chi Kristu.** Iyi ndi gulu la olakwa akale ndipo limatchedwa kuti “banja lapakati” chifukwa ndi panjira kuchokera ku ndende kubwerera kukhalanso ndi anthu. Mtundu wa utumiki uyu nthawi zambiri umaperekwa malo okhala, chakudya, ndi mwayi wa ntchito kwa mamembala ake. Mamembala amatha kukhala kumeneko mpaka atapeza mwayi wa ntchito ndi malo okhala awo awo. Magulu ena amakhala ndi makalasi a ophunzira ndipo mamembala amayenera kumalidza maphunziro onse asanakapeze kukhala kwina. Ngati mungayambitse utumiki wa banja lapakati, ndikofunikira kukhadzikitsa malamulo okhwima okhudza makhwala otsongonedza ubongo ndi kakhalidwe kabwino.

**-Utumiki wolanditsa:** Madera ena amakhala ndi utumiki wolanditsa womwe umalandira wolakwa akale mu mapologalamu awo a ophunzira ndi maphunziro ena a ntchito zamanja.

**-Mapologalamu a boma ndi anthu ena:** M'madera mwina muli mapologalamu a boma kapena a anhu omwe amathandidza olakwa akale kuti abwereretso m'madera awo. Ena mwa mapologalamuwa ndi nyumba za gulu, malo operekera uphungu, ndi zithandidzo zina.

**-Masukulu a Chikhritsu:** Ena amathandidza kulipirira ndalama za sukulu, malo okhala kwa akayidi akale. Ngati muli wamkulu wa Sukulu ya Chikhristu, uwu uthakukhala utumiki wabwino kwainu.

### **KUYAMBA UTUMIKI WA KUNJA KWA NDENDE**

Awa ndi masitepe omwe mungachite poyamba utumiki wa kunja kwa ndende:

#### **SITEPE YOYAMBA: Kupemphera**

Zinthu zonse zimayamba ndi pemphero. Pempherani zimene Mulungu angafune kuti inu muchite mu utumiki wa kunja kwa ndende.

#### **SITEPE YACHIWIRI: Kaonaneni ndi mtsogoleri wanu wa uzimu**

Ngati ndinu m'busa, kakumaneni ndi oyang'anira mpingo wanu wonse. Ngati muli membala wa mpingo, kakumaneni ndi abusa anu. Izi ndi zofunika pazifukwa zambiri:

- Ndi dongosolo yokhazikika.
- Adzitsogoleri auzimu atha kukutsogorerani ndi kupereka nzeru zofunika.
- Adzitsogoleri anu atha kukhala kuti anali kale ndi mapulani a utumiki umenewu. Ngati ziri choncho, khalani mbali ya utumikiwo, osauyang'anira pansi.

#### **SITEPE YACHITATU: Pangani kafukufuku**

Awa ndi mafunso omwe mukuyenera kuyankha pomwe mukupanga kafukufuku:

-Kodi pali ma utumiki akunja kwa ndende m'dera lanu? Ngati ziri choncho, ndi ati? (Mutha kufuna kukhala mbali imodzi ya utumiki wa kunja kwa ndende omwe alipo kale m'dera lanu)

-Kodi pali zosowa zanji zomwe zilipo mu dera lanu zokhudzana ndi utumikiwa a kunja kwa ndende

- Kodi ndizosowa zanji zomwe inu ndi/kapena mpingo wanu mungakwanitse kupereka? (Muyetsetse kuti musachite zinthu zomwe anthu ena akuchita kale. Tikuyenera kuyamikirana, osati kuchita mpikisano.)

#### **SITEPE YACHINAYI: Kuyendera utumiki wonga uwu**

Ngati mukufuna kuchita utumiki wa kunja kwa ndende, yenderani utumiki wonga uwu omwe mukuuziwa. Phunzirani mphamvu zawo ndi zofooka zawo.

**-Zachuma:** Utumiki wa kunja kwa ndende umafunikira chithandidzo cha chuma. Dzivani mmene chuma chingapedzekera.

**-Malo ochitira utumiki:** Ndi malo otani omwe mungafune kuti muzichitira utumiki? Malowo ali kuti? Kodi mungapedze chiroledzo kuchokera ku akulu akulu aboma a m'dera lomwe mukufuna kumachitira utumikiwo?

**-Ogwira ntchito:** Kodi ndi ndani yemwe adzitengapo gawo pa pologalamu yanu? Kodi ndi maphunziro otani omwe angalandire? (Mutha kugwiritsa ntchito bukuli pochititsa maphunziro. Chimenecho ndi cholina chimene bukuli linalembewera)

### **KUDZINDIKIRA UDINDO WANU**

Kodi udindo wanu ndiwotani pa utumiki wa kunja kwa ndende? Utengera ndi mayankho a mafunso osatirawa:

- 1. Kodi chomwe chimavomerezewa ndi ndende mu utumiki womwe mukutumikira ndi chani?** Ndende zina zimakanidza ogwira ntchito omgodzipereka omwe amatumikira mkaati mwa ndende kutumikira ku akayidi omwe amasullidwa. Chifukwa chake ndichakuti, ngati mkayidi angadzabwerere ku ndende atha kuwonetseredwa chikondi chapaderadera.
- 2. Kodi ndi mbali yiti yomwe muli ochita chita?** Kodi ndinu ochitachita potumikira akayidi omwe ali mu ndende kapena omwe amasulidwa? Kodi zokhumba zanu ndi masomphenya anu ali kuti? Kodi chomwe chimakupasana chimwemwe chochuluka ndi zotsatira zambiri za uzimu ndi chiti?
- 3. Kodi zotchinga zanu za nthawi ndi mphamvu ndi ziti?** Inu simungakhale chirichonse kwa wina aliyense. Chifukwa cha kuperewedwa kwa nthawi ndi mphamvu kwanu, inu mukuyenera kudzipereka ku utumiki wa akayidi omwe ali omangidwa kapena omwe amasulidwa, osati onse pakamodzi.

Ngati ndende yanu siyikukulolanu kutengapo gawo pa akayidi omwe amasulidwa kapena mulibe nthawi kapena mphamvu zopangira utumiki wa kunja kwa ndende, inu mukuyenera kugwira ntchito ngati ongopereka uphungu. Mukhale ndi mndandanda wa mipingo, anthu, kapena magulu omwe amachita utumiki wa kunja kwa ndende ndipo mudziwalondorera akayidi omwe amasulidwa kumeneko.

Kaya mwatengapo gawo lanji, udindo wanu ukuyenera kukhala uchita ubale ndi kuphunzitsa. Musakhale thandidzo la mkaidi. Mukhale opedzeka, koma musatenge udindo wa bambo kapena mayi pa moyo wake. Muwalimbukitse kuti akhale odzidalira okha.

## **MAFUNSO OZIYESA NOKHA**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Kodi zosowa za akayidi omwe atulusidwa ku ndende ndi ziti?

---

---

3. Lembani mitundu ya utumiki wa akayidi omwe atulusidwa kundende.

---

4. Lembani masitepe poyambisa utumiki wa akayidi omwe atulusidwa ku ndende.

---

5. Kodi ndi mafunso ati atatu omwe angaonetsera udindo wanu pa utumiki wa kunja kwa ndende?

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chapatala chomalidza mu bukuli)

# CHAPUTALA 10

## Mitundu ya Ndende ndi Akayidi

### VESI YOTSOGOLERA:

**Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine; pakuti Yehova wandidzoza ine ndilalikire mau abwino kwa ofatsa; Iye wanditumiza ndikamange osweka mtima, ndikalalikire kwa am'nsinga mamasulidwe, ndi kwa omangidwakutsegulidwa kwa m'ndende.**  
**(Yesaya 61:1)**

### ZOLINGA:

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kuonetsera kumvetsetsa chitedzo chakundende.
- Kufotokoza kusiyana kwapakati pa maselo, ndende ndi malo ena osungira akayidi.
- Kufotokoza mitundu ya akayidi.
- Kufotokoza momwe mungagwirire ntchito ndi akayidi omwe akuti sanapalamule.

### CHIYAMBI

Kodi akayidi ena amatengedwa oopsa kuposa ena? Kodi pali kusiyana kwa selo ndi ndende? Kodi akayidi amakhala ndi makhalidwe ofanana? Kodi mkayidi yemwe akuti sanalakwe mumamuthandidza bwanji? Izi ndi zinthu zofunikira zomwe zakambidwa mu chaputala ichi.

### MITUNDU YA NDENDE

Ndende ina ili yonse ndi yosiyanu ndi inzake, koma ndende zambiri zimasiyanisidwa chifukwa cha mitundu ya akayidi imasunga:

**-Ndende za chitedzo chokhwima:** Ndendezi zimasunga akayidi omwe ali pachiopsezo chachikulu, mwina chifukwa cha mtundu wa milandu wawo kapena makhalidwe awo. Akaidi omwe agamulidwa kukanyongedwa nthawi zambiri amasungidwa mu ndende izi. Akayidi awa amayang'anidwa kwambiri ndipo kutenga gawo ku mapologalamu ochitidwa ndi ogwira ntchito ongodzopereka nthawi zina kumaletsedwa.

**-Ndende za chitedzo chapakati:** Awa mumakhala akayidi omwe ali ndi chiwawa chochepa omwe alibe chiopsezo chochuluka kapena kuthawa. Awa safuna kuyang'anidwa kwambiri ndipo amaloledwa kutenga nawo gawo pa mapologalamu a zachipembedzo.

**-Ndende za chitedzo chochepa:** Umu mumakhala akayidi omwe ali apfupi kutulusidwa, m'ndende za milandu yopanda ziwawa, kapena omwe adzionetsera okha cuti atha kudalirika ndi kukhululupiridwa. Amathanso kumagwira ntchito

kunja kwa ndende ndipo nthawi zambiri amakhala ndi mwayi otenga nawo mbali pa mapologalamu a zachipembedzo

Ndende zina zimakhala ndi malo onse atatuwa. Nthawi zina akayidi amavekedwa mayunifolomu a mitundu yosiyana siyana m'malingana ndi malo a chitedzo omwe iwo akukhala.

### **KUSIYANA KWA MASELO NDI NDENDE**

Ingakhale muselo ndi mu ndende ndi malo a anthu olakwa, koma iwo ndi osiyana. Akayidiaku ndende ndi omwe ayesedwa ndi kugamulidwa kuti ndi olakwa. Selo ndi komwe akayidi amafikirfa akagwidwa. Akayidi ambiri omwe amakhala mu selo amakhala kuti sanapezedwe olakwa ndi mulandu wina uliwonse. Ambiri amakhala kuti akusungidwa kutikirira kukayesedwa. Ena amakhala kuti akudikirira chigamulo. Ena amakhala kuti akugwira milandu yaying'ono yomwe sakuyenerakupita ku ndende.

Chiwerengero chakundende nthawi zambiri chimakhala chokhadzikika. Anthu amakhala kuti akugwira milandu yayitali ndipo mutha kukhala ndi nthawi yabwino yogwira nawo ntchito. Chiwerengero chamu selo chimakhala chosinthsinthia. Anthu amakhala mu selo chifukwa akudikirira kuyesedwa, chigamulo, kapena akugwira mulandu wawung'ono. Nthawi yanu ndi iwo imakhala yochepa.

Ndende zambiri zimakhala ndi malo ndi mapologalamu opereka ophungu ndi kukhadzikitsidwa koma maselo ambiri alibe. Ndende nthawi zambiri zimakhala ndi malo okumaniranako gulu ngati chipembedzo cha mpingo ndi Kuwerenga Baibulo pa gulu.

### **MITUNDU YINA YA MALO OSUNGILAKO AKAYIDI**

Mitundu yina ya ukayidi ndi:

**-Nyumba ya theka:** Malo usungula akayidi omwe amasulidwa kumene. Amakhala malo amenewa pamene amakhala akudikirira kupeza mwayi wa ntchito ndi malo awo okhazikika okakhala. Amantha kuwuzidwa kuti amalidzitse kaye pologalamu ya uphungu asanachikeko.

**-Msasa wapa msewu, msasa wa moto, msasa wa munkhalango, kapena kugwira ntchito mminda:** Akyidi omwe akugwira ntchito misewu, olimbana ndi moto, kapena kugwira ntchito mu nkhalango ndi minda ya boma.

**-Ndende za ana:** Malo omwe kumakhala ana opalamula omwe amalekanitsidwa ndi akayidi akaulu akulu.

Kusatengera zovuta zomwe ziripo, ndende ndi malo omwe kuli zotuta zambiri za uzimu. Yesu anali ndi nthawi yochepa ndi chigawenga chomwe anakhomedwa nacho pamtanda koma tsogola lache linatsinda mpaka muyaya.

## MITUNDU YA AKAYIDI

Mkayidi aliyense ndi osiyana ndi mzake. Mulungu amawako akayidi onse ndipo sakufuna kuti mmodzi mwaiwo akaonongeke. Pa maso a Mulungu palibe mitundu ya akayidi, koma pali zikhaldwe zina zomwe zingakuthandidzeni kudzindikira mitundu ya akayidi:

**Maphunziro:** Nthawi zambiri, akayidi ambiri amakhala osaphunzira.

**Kakhalide kamu banja:** Nthawi zambiri akayidi amachokera m'banja omwe mumakhala nkhanza, kutha kwa banja, chisamaliro chochepa, ndi banja lopanga kulanga.

**Maphunziro azantchito:** Akayidi ambiri ali ndi maphunziro a ntchito ochepa kapena alibiretu. Amatha kukhala kuti analephura kupeza mwayi wantchito kapena kukhadzikika pa ntchito kapena kuvutika pa ntchito yomwe amalandira ndalamo zochepe.

**Kuziyang'anira pansi:** Akayidi nthawi zambiri amaziyang'anira pansi chifukwa chakukanidwa ndi anthu, abwenzi ndi mabanja awo.

**Mavuto a nkhawa:** Akayidi ambiri amavutita ponzimverachisoni chifukwa cha zomwe anachita mbuyomo kapena zomw apadanja pawo adutsamo chifukwa cha iwo. Matenda a nkhawa ndi ochuluka pakati pa akayidi.

**Milandu yofanana:** Milandu inayi yomwe ari yochuluka pakati apa akayidi ndi: Kuba kolands, Kuba m'nyumba (kuthyola nyumba), Kupha, ndi kuphwanya zinthu Kamba ka makhwala osokoneza ubongo. Zifukwa zina za ukayidi ndi kugwiririra, kuzembesa munthu, Kumenyana, kuba, ndi chinyengo.

**Kumbukirani, makhaldwe awa siwoona kwa akayidi onse.** Akayidi ena ndi ophunzira kwambiri ndipo anali ndi ntchito zapamwamba. Ena amachokera ku mabanja abwino ndi othandidza. Ena akufunadi, ndi chikhumbokhumbo chomudziwa Mulungu. Makhaldwe awa achokera pa kafukufuka wa akayidi ochuluka.

**Chofunikira kwambiri,** kumbukirani kuona mkayidi wina aliye se osati momwe analiri oyamba, kapena momwe aliri pano. Aonene ngati anthu a Mulungu aphindu omwe angakhale pamene Uthenga Wabwino wagwira ntchito mwa iwo.

## KODI AKAYIDI ENA NDIOSAPALAMULADI?

Akayidi ambiri amati ndiosalakwa. Kwa iwo omwe ndiolakwa, ichi chimakhala njira yothawira. Sangakwanise kukumana ndi zomwe anachita ndiye amawanamizira anthu ena. **Koma chonde, mukhale odzindikira, akayidi ena amene amati ndiosalakwa amakhaladi kuti ndiosalakwa!** Pali nthawi zambiri zomwe akayidi anamasulidwa atatsmikiziridwa, kuti anamandingwa popanda mulandu. (Izinzo ndizotheka kwa akayidi omwe agamulidwa kukanyongedwa!)

Inu simuli kumeneko kuti mukaweruze kulakwa ndi kulungama kwa akayidi. Inu muli kumeneko kukapaka ubale ndikutumikira chikondi cha Mulungu kwa iwo. Khalani othandidza. Awudzeni kuti mupemphera kuti Mulungu alowerere mumulandu wawo ndikuti chilungamo chiwonekere.

Kumbukirani kuti, pazifukwa zosiyanasiyana, ngwazi za chikhulupiro zambiri zinalowapo kundende. Yosefe anakhala zaka ziwiri kundende atanamiziridwa kuti amafuna kugwirrira (Genesis 39). Samusoni anamangidwa ndi Afilisti (Oweruza 16). Yeremiya anayikidwa mu ndende ya Mfumu Zekekiya kawiri, poyamba chifukwa cha kulalikira kotsutsana ndi mfumu and kena chifukwa chonamidziridwa kuti akufuna kulanda ufumu (Yeremiya 32,37).

Atuumwi ambiri anaponyedwa mundende ndi Asudoku (Machitidwe 5). Herodi anamanga Yohane M'batizi (Mateyu 4) ndi Petro (Machitidwe 12), komanso Paulo. Mntumwi Paulo anakhala kwambiri mu ndende. Anagwira ukayaidi ku yerusalem (Machitidwe 23), ku Kaisareya (Machitidwe 23), ku Filipi (Machitidwe 16), ndi nthawi zina ziwiri ku Roma.

Akhristu akhala akumangidwa mu mbiri yonse ya mpingo, John Bunyan ndi Dietrich Bonhoeffer ndi okhulupirira awiri odziwika omwe anamangidwapo. Ku China, Russia, ndi Uganda okhulupirira zikwi zikwi amamangidwa ndi kuphedwa.

Yesu anati kukhala Khristu okhulupirira kutha kupangitsa kuti umangidwe (Mateyu 10 ndi 24). Tikawonetsetsa, kukhala mkayidi kutha kubweresa kukhulupirira, ngati mmene anadzindikirira chigawenga pamtanda.

**Nthawi zonse kumbukirani**

... kuli ngwazi za chikhulupiro

Mbali zonse za ndende.

## **MAFUNSO OZIYESA NOKHA A CHAPUTALA 10**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Lembani chitedzo chakundende.

---

3. Fotokozani kusiyana kwapakati pa maselo ndi ndende.

---

4. Kodi malo ena osungulako akayidi omwe akambidwa mu chapatalachi ndi ati?

---

5. Kufotokoza mitundu ya akayidi.

---

---

6. Kodi mungagwirire ntchito bwanji ndi akayidi omwe akuti sanapalamule?

---

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chapatala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 11**

## **Malamulo A Kavalidwe Ndi Chitedzo**

### **VESI YOTSOGOLERA**

**Anthus onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wocokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu. (Aroma 13:1)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kufotokoza mavalidwe oyenera ku ndende.
- Kufotokoza malamulo za chitedzo za ku ndende.

### **CHIYAMBI**

Ndende zambiri ziri ndi malamulo zapadera dera za mavalidwe ndi chitedzo. Onetsetsani kuti mwafufuza za izi, ndipo pemphani izi kuti akulemembereni ngati ziripo. Mu chaputala ichi, muphunzira malamulo za kavalidwe ndi chitedzo za ku ndende

### **KAVALIDWE KOYENERA**

Ndende ina iriyonse ili ndi mavalidwe akeake. Mwachitsanzo, ndende zina zimakaniza ogwira ntchito yongozipereka ndi ozaona akayidi kuvala zovala za mitundu yofanana ndi mitundu ya zovala za akayidi ndi ogwira ntchito ku ndende. Onetsetsani kuti mwafunsa za kavalidwe ku ndende komwe mukufuna kukachita utumiki. Izi ndi zina mwa malamulo akavaldwe koyenera ka ku ndende:

- Musavale zovala zothina kwambiri.
  - Musavale zovala zomwe zalembenza mawu omwe atha kutanthauzidwa molakwika.
  - Musavale zovala zowonekera m'katu.
  - Musavale kabudula
- Kwa azimayi**
- Ngati zovala zazifupi, zovala zonse zizidusa m'maondo.
  - Musavale zovala zowonekera m'katu.

Kulankhula momveka bwino, muvale zovala zomwe ziri zoyenera kuvala ku malo a ntchito. Inu muli kumeneko kukagwira ntchito ya Mfumu ya Mafumu!

“Ogwira ntchito yongozipereka wabwino nthawi zonse amasatira malamulo a ku ndende komwe akugwirako ntchito. Malamulowo atha kukhala ngati opusa, koma iye amakhala okondwa kuwamvera. Ogwira ntchito modzi atha kuononga pologalamu yonse pakusamvera malamulo.” M’busa wa kundende

## **MALAMULO A CHITETEDZO**

Ndende ina iriyonse ili ndi malamulo a chitetedzo. Onetsetsani kuti mwafunsa za malamulo a ndende yomwe mukufuna kukachita utumiki. Kumvera malamulo kuzapangisa kuti umboni wanu wach khristu ukhale womveka ndi kupangitsa utumiki wanu kukhala ochitachita. Phunzirani ndi kumvera malamulo onse a ku ndende komwe mukutumikira.

Awa ndi malamulo omwe a ku ndende:

1. Siyana zinthu izi kunyumba kwanu kapena mugalimoto mwanu: Zikwama (pesi, waleti, bulufikesi), ndalamu ndi china chirichonse chomwe simukagwirisa ntchito ku ndende.
2. Nthawi zonse muzinyamula chindindikiro chanu. Ndende zambiri zimafuna kuti pachndindikiro chanu padzikhalapo nkhopre yanu.
3. Nthawi zonse muzikhala okonzeka kuti mukamvera kufufufuzani.
4. Kumanani ndikufikira limodzi ngati mukutumikira ngati gulu.
5. Muonetsetse kuti mukumvera malamulo akavaldwe.
6. Nthawi zonse funsani m’busa wakundende kapena ogwita ntchito kundende ngati musakumvetsetsa.
7. Ngati mukutumikira ngati gulu, maso anu azikhala pa wina ndi mzake.
8. Musathamange mu ndende.
9. Musalowe malo onse omwe ali oletsedwa kulowako.
10. Mudziwe ndondomeko zapangozi.
11. Ngati pakufunika chithandidzo chamankhwala kwa mkwayidi amene mukumutumikirayo, dziwani ndondomeko yomwe mukuyenera kutsata poyitanitsi chithandidzo.
12. Ngati upandu wachitika...
  - Itanani thandidzo mwansanga.
  - khalaniodekha komanso ndikudekhesanso ena
13. Musatenge katundu wina aliyense woletsedwa kulowesa mu ndende
14. Musatenge mankhwala ena ali wonse kulowesa mu ndende.
15. Musatenga makamera kulowesa mu ndende.
16. Musasiye chovala chanu pamalo omwe chingatengedwe ndikugwiritsidwa ntchito ndi akayidi.
17. Ngati mwapasidwa makiyi, asungeni pamalo abwino.
18. Maofisala omwe amakhala pa khomo lolowera ku ndende amakhala ndi mphamva yofufuza katundu wina aliyense mu galimoto mwanu, chonde musawakanize.
19. Musatenge uthenga kuchokera kunja kupitisa kwa akayidi.

20. Ndende zambiri zimapereka ma kadi achidzindikiro. Onetsetsani kuti mwaivala kapena kuyinyamula nthawi zonse muli mu ndende.

**Zindikirani:** Chonde musalole kuti zokambirana za chitedzochi zikukubwezereni mbuyo pa utumiki wa ku ndende. Nthawi zonse pepherani mulimphika ndi kudalira Mzimu Woyer. Dzindikirani kuti palibe chomwe chimachitika popanda Mulungu kuikapo dzanja. “Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace. (Aroma 8:28)

## **MAFUNSO OZIYESA NOKHA A CHAPUTALA 11**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Fotokozani mavalidwe oyenera ku ndende.

---

3. Lembani malamulo za chitedzo za ku ndende.

---

---

---

4. Tengani mndandanda wa malamulo a kavalidwe ndi chitedzo a ndende yomwe mukuyendera kapena kutumikira. Ikani izi mu gawo lomaliza (Chaputala 13) la bukuli.

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 12**

## **Kupanga Ubwenzi Ndi Akayidi**

### **VESI YOTSOGOLERA:**

**...wolangiza iwo akutsutsana mofatsa; ngati kapena Mulungu awapatse iwo citembenuziro, kukazindikira coonadi, ndipo akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace. (2 Timoteo 2:25-26)**

### **ZOLINGA:**

Pomaliza pa punzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kufotokoza lamulo loyamba popanga ubwenzi ndi akayidi.
- Kulemba machidule malangizo opangira ubwenzi ndi akayidi.

### **CHIYAMBI**

Ngati membala wa utumiki wa kundende, mukuyimirira Yesu Khristu, osati nokha. Ndinu Kazembe wake. Kudzera mu zichitochito zanu, mawu ndi/kapena kavalidwe, mutha kundzndidza kapena kuphinja ntchito ya Mpingo wake ku ndende.

Kumanga ubwenzi sichinthu chophweka kunja kwa ndende ndipo mu ndendenso ndikovuta. Akayidi ena atha kukhal osasangalatsidwa ndi zinthu zauzimu. Ena kukukanani. Ena atha kukugwiritsani ntchito pofuna kупедза зосова заво. Zitha kuthandidza kukumbukira fanizo la Yesu la wofesa mbewu ndi mitundu inaya ya nthaka pomwe mbewu zinagwerapo. Akayidi, ngati wina aliyense, akakhala mu mbali imodzi ya izo. Chaputala ichi chikupereka malangizo omwe munapangire ubwenzi ndi akayidi mu ndende.

### **LAMULO LOYAMBA**

Lamulo loyamba popanga ubwezi ndi akayidi: Phunziranui ndi kutsatira malamulo onse aku ndende komwe mukutumikira: Malamulo ngati nthawi yowonera, amene angalowe ndi amene sangalowe, zomwe zingalowetsedwe, komwe mungapite ndi komwe simungapite, ndi mavalidwe. Chaputala 11 cha bukuli chikukamba zambiri za malamulo a mavalidwe ndi chitedzo omwe sangakambidwenso pano. Chaputala ichi chikukamba za kupanga ubwenzi ndi akayidi ndi zochitika zag ulu.

### **MALANGIZO OPANGIRA UBWENZI NDI AKAYIDI**

Akayidi akumana ndi kukhumudwitsidwa kwakukulu pa moyo wawo. Ambiri akhala akukumana ndi kulephera mobwerezabwereza ndipo amakhala okayikira mwaiyi winauliyonse chachithandidzo kapena chitsogozo. Zotsatirazi ndi malangidzo omwe mungatsatire pamene mukupanga ubwenzi ndi akayidi:

- Mutsazipangire dzina inu nokha. Mulole kuti akayidi akudziweni chifukwa chakudzitsegula mtima kwanu. Mukhale achilungamo, akayidi amakhala nthawi zonse okayikira ku chinyengo.
- Muphunzire zilankhulo zomwe zimagwiritsidwa ntchito kundende mwachangu, koma mukhale otsamala kagwiritsidwe kake katchito.
- Muphunzire kuperekwa uthenga wachipulumutso momveka bwino.
- Muzitanthauza chomwe mukunena. Eya ndi eya, ayi ndi ayi.
- Mukhale othandidza, oona mtima ndi okhadzikika.
- Ulemu ndi kiyi. Mukuyenera kuwapasa ulemu akayidi.
- Osaziganizira nokha kuti mkayidi ndi osalakwa kapena ndi olakwa ndipo musapereke uphungu wamalamulo. Inu si omuyimilira pa mulandu kapena oweruza milandu.
- Muziperekwa malonjezo okhawo omwe mukudziwa kuti mukwaniritsa.
- Osamaperekwa adiresi ya malo omwe mumakhala kapena numbala la lamya yanu.
- Osatengapo nawo gawo popanga malonda ndi akayidi.
- Osadabwa kapena kukhumudwa ndi chinachirichonse chimene mkayidi anganene kapene mmene angachirnkhulire.
- Osawakopa akayidi kuti absinthe chipembedzo chawo. Muli kumeneko kugawa Uthenga Wabwino, osati kufalisa mpingo wanu.
- Zipatseni nokha ulemu.
- Osatenga mavuto a mkayidi painu. Iwo si mavuto anu.
- Muzikhala ndi malire. Akayidi ena atha kukukakamizani mpaka mutanena kuti musiye. Momwe angakukankhireni zimatengera kuti mwayika malire anji.
- Osachita mantha pamene mwasala nokha ndi mkayidi.
- Osaonetsera kuti mwakwiyitsidwa ndi zomwe mkayidi walankhula.
- Mukhale omvetsera bwino. Simukuyenera kuyankha chirichonse, koma muwaonetse kuti Mulungu amatha.
- Khaladi odekha.

## **MAFUNSO OZIYESA NOKHA**

1. Lembani vesi yotsogolera.

---

2. Fotokozani lamulo loyamba popanga ubwenzi ndi akayidi.

---

3. Lembani machidule malangizo opangira ubwenzi ndi akayidi.

---

(Mayankho a mafunso oziyesa nokha aperekedwa ku mapeto kwa chaputala chomalidza mu bukuli)

# **CHAPUTALA 13**

## **Malangizo**

Bukulu likupereka malangizo omwe amagwira ntchito ku ndende zonse. Koma gawo lomalidza lino likupereka malingizo a kundende komwe inu mukachitireko utumiki.

Awa ndi ena mwa zinthu zomwe mutha kuphatizika mu gawo iri la bukuli:

- Tchati cha bungwe la utuiki wanu wa kundende ndi/kapena cha ndende yomwe inu uzikatumikira. (Tchati cha bungwe chimaonensa amene ali mbali ya utumiki wanu ndi amene mukuyenera kugwira naye ntchito ku ndende.)
- Malamulo akazalidwe ndi chitedzo cha ndende yanu.
- Malangizo apadera dera a momwe muziwayendera akayidi, kuphatikiza matsiku, ndi nthawi oyoyendera akayidi, ndi zinthu zomwe mutha kutenga kapena osatenga.
- Malangizo olinganizisana ndi akayidi ndi zinthu zomwe zingathe kutumizidwa kudzera pa kalata.
- Mapu a ndende.
- Zoperekpa pa maphunziro omwe aperekedwa ndi ndende.
- Mndandanda wa ma bungwe omwe kapena mautumiki omwe omwe amathandida akayidi omwe angomasulidwa kumene ndi malo okhala, mwayi wa ntchito, zovala, zachuma, ndi zina zambiri.
- Ngati ndinu m'busa kapena wam'kulu wa antthu ogwira ntchito mongodzipereka ndipo mwakonza zinthu zophunzitsira ku ndende yanu, ikani zinthuzo mu gawo ino.
- Ngati ndinu mphunzitsi waku sukulu ya Baibulo, ikani zomphunzitsira zanu u gawo ino.

# POMALIZA

**... koma mau a Mulungu samangika. (2 Timoteo 2:9)**

Yesu ali mu ndende yanu. Akuchita nthawi mu ndende...

**“Pomwepo olungama adzamyankha Iye kuti, Ambuye, tinakuonani Inu liti ...  
kapena m’nyumba yandende, ndipo tinadza kwa Inu? Ndipo Mfumuyo idzayankha  
nidzati kwa iwo, Indetu ndinena kwa inu, Cifukwa munacitira ici mmodzi wa abale  
anga, ngakhale ang’onong’ono awa, munandicitira ici Ine.” (Mateyu 25:37-40)**

Pakuona mu uzimu, palibe mtengo omwe ungayikidwe pa moyo wa munthu:

**“Pakuti munthu adzapindulanji, akalandira dziko lonse, nataya moyo wace?  
kapena munthu adzaperekANJI cosintha ndi moyo wace?” (Mateyu 16:26)**

Pakuvomereza lamulo la utumiki wa kundende, mukupita kunsi kwa gahena komwe kuli miyoyo ya mtengo wapatali pamaso pa Ambuye.

Inde, akhalapo ena omwe salandira uthenga wanu. Ena auvomereza koma otsaulandira mu mtima mwawo. Ena azabwerera ku ntchito zavo zakale. Kom kumbukirana...

-Mulungu anayamba ndi anthu (Adamu ndi Hava) omwe anali ndicholowa chaungwi omwe makhala mu malo aungwi, koma onse analephera.

-Pamene Yesu anabvumbulutsa kuti akuyenera kuvutika, ophunzira ambiriri analeka kumutsatira, iwo sanali okonzeka kupereka mtengo wake.

-Mu maola Ake otsiriza, ophunzira aka otsala anathawa, m’modzi anamukana kuti sakumuziwa, ndipo m’modzi anamupereka, koma ambiri ayiwo anakwaniritsa ntchito yayikulu yotengera Uthenga Wabwino ku mitundu yonse ya dziko lapansi.

Musayese kufunika kwa utumki wa kundende ndi zolephera zanu. Muyese kufunika kwanu ndi chipambano chanu. Inu muli mbali ya anthu omwe akusintha dziko lapansi, ndende imodzi pa nthawi ndi mkayidi m’modzi pa nthawi.

Pali zovuta zambiri zautumiki wa ku ndende, komanso pale mphoto zapamwamba dzedi. Ogwira ntchito nthawi zambiri amayamba kugwira ntchito ndi akayidi ndi olakwa akale akuganiza kuti, “Ine ndipita kumalo a mdimaku ndi kupitisako chikondi cha Mulungu.” Koma nthawi zochepa, ambera akuchitira umboni kuti, “Ndinalandira zochuluka kuponsa zomwe ndinapereka.”

Pakuvomereza utumki wa ku ndende mumakhaa mbali ya gulu losangalala, gulu la padziko lapansi lomwe likututa miyala ya mtengo wapatala kwa Atate.

**Ndipo adzakhala anga anga, ati Yehova wa makamu, tsiku ndidzaikalo, ndipo  
ndidzawaleka monga munthu aleka mwana wace womtumikira. (Malaki 3:17)**

Pitilizani kukuza ana auzimu mpaka Atate azabwere:

- Ine musabwezedwetsedwe mbuyo.
- Musataye masomphenya
- Musamusiye mkayidi panjra.
- Musasiyire pa njira.

**Tukula maso ako uunguze-unguze ndi kuona; iwo onse asonkhana pamodzi, adza kwa iwe; ana ako amuna adzacokera kutari, ndi ana ako akazi adzaleredwa pambali. (Yesaya 60:4)**

# ZAKUMAPETO

## Malembo okhudzana Ndi Akayidi

|                           |  |
|---------------------------|--|
| Genesis 39:11-41:41       | Yosefe kunamidziridwa kuti amafuna kugwiririra ndi zokumana nazo ku ndende.                    |
| Genesis 42:15-20          | Yosefe kumanga abale ake.  |
| Genesis 45:4-8            | Yosefe adziulula yekha kwa abale ake.  |
| Numeri 21:1:              | Mfumu Aradi imanga ena mwa a Israyeli.   |
| Oweruza 16:21-25          | Samusoni achotsedwa maso ndi kumangidwa.   |
| 1 Mafumu 22:27            | Mika amangidwa chifukwa cha uneneri wake.  |
| 2 Mafumu 17:4             | Hosheya, Mfumu ya Israyeli amangidwa ndi mfumu ya Asiriya chifukwa choukira                    |
| 2 Mbiri 16:7-10           | Mneneri Hanani anamangidwa ndi Asa Mfumu ya Ayuda chifukwa chakuperekwa uneneri woypa.         |
| 2 Mbiri 18:26             | Mikaiya kumangidwa ndi Ahabu, Mfumu ya Yuda chifukwa cha uneneri wake                          |
| Maslimo 69:33             | Ambuye sanyoza akayidi   |
| Masalimo 79:11 ndi 102:20 | Pempho kwa Ambuye kuti atetedzo omwe aweruzidwa kuti aphedwe                                   |
| Masalimo 146:7            | Ambuye amamasula andende.  |
| Yesaya 14:17              | Satana salola kuti andende ake amasulidwe.   |
| Yesay 24:21-22            | Mafumu a dziko lapansi amangidwa   |
| Yesaya 42:7               | Uneneri wa kubwera kwa Yesu kuzamasula andende.  |
| Yesaya 61:1               | Kulengedzedwa kwa odzodzedwa wa Ambuye odzakhadzikitsa ufulu kwa omangidwa                     |
| Yeremiya 32:1-2           | Kumangidwa kwa Yeremiya ku Yada  |
| Yeremiya 32:6-15          | Yeremiya agula munda pomwe ali ku ndende   |
| Yeremiya 33:              | Ambuye alankhulana ndi Yeremiya pomwe iye ali ku ndende  |
| Yeremiya 40:1-4           | Yeremiya athawisidwa ku ndende   |
| Yeremaya 52:11            | Zedekia mfumu ya Yerusalem, amangidwa ndi mfumu yak u Babelo                                   |
| Maliro 3:34               | Mulungu saponderedza andende   |
| Maliro 3:53-34            | Yeremiya adandaulira Yehova ali ku ndende  |
| Danieli 3:1-28            | Shaderk, Misheki, ndi Abidnego amangidwa, ndikuponyedwa mu ng'anjo ya moto ndi kupulumutsidwa. |
| Zekariya 9:11-12          | Mulungu alonjeza kupulumutsa andende   |
| Mateyu 4:12               | Yohane m'batizi amangidwa  |
| Mateyu 5:25-26            | Langizo lokuti ndikwabwino kufulumira kuyanjana ndi mzako wapamulandu.                         |
| Mateyu 11:2               | Yohane m'batizi, yemwe ali mu ndende, afunsa Yesu ngati ali Yemwe amayenera nkuza              |
| Mateyu 14:3,10            | Yohane m'batizi amangidwa, ndikudulidwa mutu   |
| Mateyu 18:30              | Kapolo opanda chifundo ayika mzake yemwe ali naye ngongole mndende                             |

|                           |   |
|---------------------------|---|
| Mateyu 25:35,39,44        | Yesu anena kuti anthu omwe amatumikira ku ndende amatumikira kwa Iye ndi kuti anthu omwe sakutumikira kundende akuyenera kuyamba kutumikira |
| Mateyu 27:15-21           | Barabasi amasulidwa   |
| Marko 1:14; 6:17,27       | Yohane m'batizi amangidwa ndi kugulidwa mutu  |
| Marko 15:6:               | Barabasi amasulidwa   |
| Luka 3:20                 | Yohane m'batizi amangidwa   |
| Luka 4:18                 | Yesu akamba za utumiki wake, kukwaniritsidwa kwa Yesaya 61:1-3  |
| Luka 12:58-59             | Langizo loyanjana ndi adani anu   |
| Luka 21:12-13             | Yesu awudza ophunzira ake kuti amangidwa  |
| Luka 22:33                | Petro anena kuti ali wokonzeka kutsatira Yesu ku ndende ndi imfa  |
| Petro 23:19,25            | Kumasuliidwa kwa Barabasi   |
| Machitidwe 4:3            | Petro ndi Yohane amangidwa  |
| Machitidwe 5:18-23        | Atumwi amangidwa keneno namafulidwa ndi mngelo wa Ambuye  |
| Machitidwe 5:40           | Atumwi amenyedwa chifukwa chotumikira dzina la Yesu   |
| Machitidwe 7:54-60        | Sitifano agendedwa miyala   |
| Machitidwe 8:3; 9:2,14,21 | Saulo azunza Akhristu, kutembenukaz kwake ndi utumiki wake  |
| Machitidwe 12:1-2         | Yakobo, m'bale wa Yohane, aphedwa.  |
| Machitidwe 12:3-17        | Petro amangidwa ndi kumasuliidwa ndi mngero wa Ambuye   |
| Machitidwe 12:18-19       | Herodi apha alonda omwe amayang'anira Petro   |
| Machitidwe 14:19          | Paulo agendedwa miyala ndi anthu ndipo ayetsa kuti wafa   |
| Machitidwe 16:25-39       | Paulo ndi Sila amenyedwa namangidwa   |
| Machitidwe 20:22-24       | Paulo aneneratu za kumangidw kwake ku Yerusalem.  |
| Machitidwe 21:11          | Agabasi, mneneri, atsimikidza kuti Paulo akamangidwa ku Yerusalem   |
| Machitidwe 21:30-35       | Khamu la anthu mu Yerusalem ligwira Paulo ndicholinga chofuna kumupha. Paulo apulumutsidwa ndi asilikali achiroma                           |
| Machitidwe 22:24-29       | Paulo achitira umboni kuti poyamba ankazunza akhristu   |
| Machitidwe 23:1-35        | Paulo alankhula pakati pa akulu akulu a mpingo ndipo amangidwa  |
| Machitidwe 27:1-28:15     | Ulendo wa Paulo waku Roma ali m'manja mwa asilikali achi Roma   |
| Machitidwe 28:17-20       | Paulo akamba za kumangidw kwake   |
| Machitidwe 28:16          | Paulo aloledwa kukhala mu nyumba mwake ndi mulonda womuyang'anira   |
| 2 Akorinto 11:23          | Paulo akamba za kumangidw kwake ndi zophinja zomwe wakumana nazo chifukwa cha Khristu   |
| Aefeso 3:1; 4:1           | Paulo anena kuti iye ndi kapolo wa Khristu  |
| Aefeso 6:20               | Paulo anena kuti iye ndi Kazembe womangidwa   |
| Afilipo 1:11-18           | Paulo anena kuti kumangidw kwake kwapititsa patsogolo uthenga wa Khristu  |
| Akolose 4:10              | Aistaasi ndi womangidwa limodzi ndi Paulo   |
| 2 Timoteyo 1:8            | Paulo awauza anthu kuti asachite manyazi chifukwa cha kumangidw kwake   |

|                     |  |
|---------------------|--|
| 2 Timoteyo 1:16-17  | Paulo adalitsa Onesifolasi chifukwa chomutumikira iye ali ku ndende            |
| 2 Timothy 2:9       | Paulo anena kuti nagkhale iye ali omangidwa, koma Mawu a Mulungu si omangidwa  |
| 2 Timothy 4:16-17   | Ambuye ayima ndi Paulo pamene aliyense anathawa chifukwa cha kumangidwa kwacha |
| Filimoni 1:9-10     | Paulo apempha chifundo pa Onesimus yemwe anapulumutsidwa mu ndende.            |
| Filimoni 1:23       | Epafulasi, omangidwa liimodzi ndi Paulo  |
| Ahebri 13:3         | Kumbukirani iwo omwe ali mu ndende nagti kuti inu mwamangidwa nawo limodzi     |
| 1 Petro 3:19        | Khristu amatumikira kwa iwo ali mu ndende                                      |
| 2 Petro 2:4         | Mulungu anamanga angelo omwe anamuukira  |
| Yuda 1:6            | Mulungu anamanga angelo omwe anamuukira  |
| Chibvumbulutso 2:10 | Satana adzamanga ena ndicholinga chofuna kuwayetsa                             |
| Chibvumbulutso 2:13 | Antipasi, wochitira umboni wa Mulungu, aphedwa                                 |
| Chibvumbulutso 20:7 | Satana atultsidwa ku ndende ka kanthawi kochepa                                |

# **MAYANKHO A MAFUNSO OZIYESA NOKHA**

## **CHAPUTALA 1**

1. .... ndinali m'nyumba yandende, ndipo munadza kwa Ine. (Mateyu 25:36)
2. Chitsanzo chachikulu cha lamulo la m'malemba la utumiki wa kundende ndi Mateyu 25:31-40.
3. Yesu ndi chitsanzo chathu chachikulu cha m'Baibulo.
4. Zifukwa zisanu ndi zinayi zimene okhulupirira akuyenera kutenga mbala pa utumiki wa kundende ndi:
  1. Chifukwa utumiki waku ndende uli ndi ulamuliro wa malembo (Mateyu 25:31-40).
  2. Tiuyenera kutsatira chitsanzo chomwe Yesu anayika pakutumikira a mndende.
  3. Ndende zimafikira muyeso wa malo onse otumikirako: Anthu otayika ndi kufunika kwa ogwira ntchito.
  4. Mulungu sakufuna kuti wina aliyense atayike--ingakhale zigawenga, ogwiririra, kapena ambanda (2 Peter 3:9). Mulungu amakonda ingakhale munthu “wochimwitsitsa” (1 Timoteo 1:15).
  5. Azibusa akundende sangatumikira oposa omwe anapatsidwa kuti adziwasamalira. Sanachite ntchito yonse yomwe ikufunikira okha, pakuti palibe nthawi yokwanira yochitira idzi.
  6. Ndende zambiri ziribe azibusa odziwa bwino ntchito yawo ndipo zilibe misonkhano ya chipembedzo.
  7. Munthu wina aliyense wamangidwa, pali anthu ambiri omwe amakhudzidwa: akayidi, ana, makolo, ndi ena ambiri. Akayidi ndi mabanja awo amayimira gawo lalikula la anthu mu mtundu wina uliwonse.
  8. Dzipembedzo zonyenga ndi amatsenga akufikira a ndende. Tikuyenera kukafikako mwachang ndi Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu!
5. Zolinga za utumiki wa kundende ndi:
  - Kugawa chikondi chopanda mangawa cha Mulungu
  - Kukapereka Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu mu nira yoti upangitse akayidi kuwulandira ndi kuvomeredza Yesu ngati Mpulumutsi
  - Kukaphunzitsa okhulupirira atsopano Mawu ndi kuwaphunzitsa mmene angamawerengere Baibulo.
  - Kukaonetsera mphamu ya pemphero ndi kuwaphunzitsa kupemphera.
  - Kuwatengera akayidi kuti akakumane ndi mphamu ya Mulungu yotsintha moyo yomwe ingawamatsure kuti maganidzo odzimvera chitsoni kuti iwo ndi wolakwa, manyazi, ndi maganizo otsakhala bwino, ndi zilakolako za zinthu zoyipa.

-Kutumikira mabanja a akayidi.  
-kuthandiza akayidi kukhala moyowabwino.  
-kupereka chithandidzo kwa akayidi omwe atuluka ku ndende.

6. Uthenga wabwino umapereka ka akayidi:

-Kukhululukidwa kwa machimo.  
-Mwayi onena kuti “pepani”  
-Kumasulidwa kuchokera ku ukapolo ndi chitonzo.  
-Kulandiridwa--pamene ambiri aiwo chomwe akudziwa ndi kukanidwa.  
-Makhalidwe ndi kachitidwe ka zinthu katsopano  
-Njira zothanira ndi nyengo zovuta ndi maganizo olakwika.  
-Moyo wochulukwa kudzera mwa Yesu Khristu.  
-Cholina chatsopano cha moyo.  
-Moyo wosatha.

## **CHAPUTALA 2**

1. ... komatu khala citsanzo kwa iwo okhulupira, m'mau, m'mayendedwe, m'cikondi, m'cikhulupiro, m'kuyera mtima. (1 Timoteo 4:12)
2. Onani yankho lanu molinganiza ndi ziyanetsero za uzimu za utumiki wa kundende zomwe zakambidwa mu chaputala ichi
3. Mbali zinayi zofunika kukonzekera bwino pa utumiki wa kundende ndi:
  1. Kukinzekera mu pemphero
  1. Kukonzekera mu mawu
  1. Kukonzekera pa ma udindo anu
  1. Kukonzekera za malo omwe mukupitako

## **CHAPUTALA 3**

1. Koma awa ndiwo anthu olandidwa zao ndi kufunkhidwa; iwo onse agwa m'mauna, nabisdwa m'nyumba zakaidi; alandidwa zao, palibe wowapulumutsa; afunkhidwa ndipo palibe woti, Bwezerani. (Yesaya 42:22)
2. Fanizitsani mayankho anu ndi masitepe oyambitsira utumiki wa kundende omwe akambidwa mu chaputala ichi.
3. Mautumiki osiyana siyana omwe mungapereke ku ndende ndi:

-Kuchititsa mapemphero.  
-Kugwira ntchito ya abusaaku ndende pamene adwala kapena ali ku tchuthi.

- Kupereka mapologalamu a machimbidwe kapena zisuzo apaderadera.
- Kuchita ma pologalamu osanthula Baibulo.
- Kupereka ma Baibulo.
- Kuonetsa kanema wa uzimu.
- Chitani ma pologalamu okumana ndi m'modzi m'modzi
- Perekani maphunziro a Baibulo.

4. Njira zolembera ogwira ntchito ndi:

- Ikani chidziwitso ku mpingo.
- Lengedzani mu mpingo.
- Pangani maposita ndikuwamata m'malo ofunikira mu mpingo wanu.
- Chitani “Tsiku la Utumiki wa ku ndende” mu mpingo kapena mipinggo yomwe mukufuna itengepo gawo pa utumiki waku ndende

5. Fanizani yankho lanu ndi zomwe zakambidwa mu chaputalachi.

#### **CHAPUTALA 4**

1. Izi ndakulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu. (1 Yohane 5:13)
2. Zinthu ziwiri zofunikira kuchitpo pomwe mukufuna kuyamba kulinganiza ndi akayidi:

- Lumikidzanani ndi akulu akulu aku ndende
- Pedzani malamulo a momwe anthu amalumikidzirana ndi akayidi ku ndende imeneyo

3. Fananizani yankho lanuu ku malangizo olinganizana ndi akayidi omwe aperekedwa mu chaputala ichi.

#### **CHAPUTALA 5**

1. Kumbukilani am'nsinga, monga am'nsinga anza; ocitidwa zoipa, monga ngati inunso adatero nanu m'thupi. (Ahebri 13:3)
2. Kuyendera akayidi ndikofunikira chufukwa:

- Moyo wina uliwonse ndi wa mtengo wake kwa Mulungu
- Akayidi ambiri sangakumane nawo m'kumanano ya chipembedzo
- Akayidi ambiri sanakumane ndi ubale woona, wa Umulungu, ndi wosaona nkope
- Mwa ambiri aife--ndikosavuta kumasuka pokamba ndi munthu kusiyana ndi ku gulu

- Inu mumakhala chowalumikidzitsa kubwerera kwa athu. Azakhala ndi m'bale owadikirira akadzatulutsidwa.
- Munthu modzi sangakhale ndi abale ambiri. Inu simungokhala m'dalitso, koma mudalitsika ndi ubale wanu ndi mkayidi.

3. Mutha kutengapo gawo pa utumiki woyendera modzi modzi mu njira zotsatirazi:

- Funsani za pologalamu yowonera akayidi ku ndende yomwe mukufuna kutengapo gawo.
  - Ngati alibe pologalamu yokhadzikika, afunseni abusa akundende kuti akulumikidzitseni ndi mkayidi. Ngati palibe m'busa, kumanani ndi wamkulu woyang'anira ndendeyo.
  - Anthu amene akutumikira m'busa, kumanani ndi wamkulu woyang'anira ndendeyo.
  - ngati kuli kotheka sinthanani makalata ndi mkayidiyo musanayambe kukumana.
- Mukhala kuti mwapanga kale ubale mukamazakumana koyyamba.

4. Fanizani yankho lanu ku malangizo omwe patsidwa mu chapatalachi.

## **CHAPUTALA 6**

1. Koma Iye, poona makamuwo, anagwidwa m'mtima ndi cisoni cifukwa ca iwo, popeza anali okambululudwa ndi omwazikana, akunga nkosa zopanda mbusa. (Mateyu 9:36)
2. Mitundu ina ya mautumiki ma magulu omwe angachitikire kundende ndi:

- Mikumano ya kulambira
- Kusanthula Baibulo
- Makalasi azamayimbidwe (Kuphunzitsa oyimba, kapana kapena kwaya ya chipembedzo chakulambira cha kundende)
- Mikumano ya mayimbidwe ndi zitsunzo.
- Zolemba zachi Khristu
- Magulupo ang'ono ang'ono opereaka chithandidzo cha chikristu kwa akayidi omwe ali ndi mavuto a chilakolako ndi nkawa.
- Maphunziro a Baibulo
- Makalasi a ophunzira a okhulupirira atsopano

3. Fananizani yankho lanu ndi malangizo omwe aperekedwa mu chapatalachi.

## **CHAPUTALA 7**

1. "... ndipo mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a dziko lapansi." (Genesis 12:3)
2. Pamene membala wa pa banja wamangidwa, nthawi zambiri izi zimalenga nkawa, mantha, ndi kusakhadzikika kwa apabanja awo, ana kapena makolo. Kumangidwa kumabweresa mavuto a akulu pa banja.
3. Mutha kutumikira ku ma banja a akayidi munjira zotsatirazi:

4. Zinthu ziwiri zofunikira zomwe mukuyenera kuchita musanayambe kulumikidzana ndi banja la mkayidi ndi:
  1. Fufuzani kwa abusa aku ndende or akulu akulu aku ndende kumene mukutumikira.
  2. Katengeni chiloledzo cholembedwa kwa mkayidi kuti banja lake ndi andende adziwe kuti muli ndi chivomeredzo chake.
5. Fananizani yankho lanu ndi malangizo omwe aperekedwa muchapatala ichi.

## **CHAPUTALA 8**

1. Kubuula kwa wandende kufike kuli Inu; Monga mwa mphamvu yanu yaikuru lolani ana a imfa atsale. (Masalmo 79:11)
2. Fananizani yankho lanu ndi maganizo omwe aperekedwa mu chapatalachi.
3. Fanizani mayankho anu ndi malangizo omwe aperekedwa mu chapatala ichi.
 

-Kodi alipo omwe akuyenera kuwapepesa ndikupempha chikhululukiro chawo—ozunzidwa, mabanja awo, banja lake kapena abwenzi ake? Athangatireni kutero.

-Ngati ali ndi ana achichepere alimbikitseni kuti awalembere kalata yomwe ingadzapatsidwe kwa iwo akazakula.

-Kambiranani nawo za imfa yawo, ndipo chilungamo choti ali okhulupirira, palibe chinthusi choti achite nacho mantha.

## **CHAPUTALA 9**

1. ...kuti utsegule maso akhungu, uturutse am'nsinga m'ndende, ndi iwo amene akhala mumdimba, aturu ke m'nyumba ya kaidi. (Yesaya 42:7)
2. Zosowa za olakwa akale ndi:

-Akuyenera kuti alandiridwe mu mpingo wakudera komwe amakhala omwe unamusamale ndi kumuthandidza kuti akule mu uzimu.

- Akusowa malo okhola, chakudya, ndi zovala.
- Akusowekera maphunziro a ntchito za manja ndi/kapena kupeza ntchito.
- Uphungu wa banja ndiwofunika ngati akufuna kuti alumikidzanenso ndi banja lake.
- Atha kusowanso uphungu wapaderadera kuzilakolako za mankhwala ozungudza umbongo.

-Ngati anamangidwa kwa nthawi yayitali, atha kufuna chithandidzo ngakhale pa zinthu zowoneka zazing'ono chifukwa akayidi amakhala ndi mwayi wochepa wopanga chisankho.

-Akusowekera abale omwe ali olimba kuti adzimukonda ndi kumulandira, kupemphera naye ndi kumupempherera, ndi kumuthangatira kuti athane ndi zovuta zomwe zingadze.

3. Ma utumiki a kunja kwa ndende ndi:

- Banja la lakati la chi Kristu.
- Utumiki wolanditsa
- Mapologalamu a boma ndi anthu ena
- Masukulu a Chikhritsu

4. Masitepo oyambitsira utumiki ka kunja kwa ndende:

- Sitepe Yoyamba: Kupemphera
- Sitepe Yachiwiri: Kaonaneni ndi mtsogoleri wanu wa uzimu
- Sitepe Yachitatu: Pangani kafukufuku
- Sitepe Yachinayi: Kuyendera utumiki wonga uwu
  - Zachuma
  - Malo ochitira utumiki
  - Ogwira ntchito

5. Mafunso atatu omwe amasonetsera undindo wanu pa utumiki wa nkunja kwa ndende:

1. Kodi chomwe chimavomerezewa ndi ndende mu utumiki womwe mukutumikira ndi chani
2. Kodi ndi mbali yiti yomwe muli ochita chita?
3. Kodi zotchinga zanu za nthawi ndi mphamvu ndi ziti?

## CHAPUTALA 10

1. Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine; pakuti Yehova wandidzoza ine ndilalikire mau abwino kwa ofatsa; Iye wanditumiza ndikamange osweka mtima, ndikalalikire kwa am'nsinga mamasulidwe, ndi kwa omangidwakutsegulidwa kwa m'ndende. (Yesaya 61:1)
2. Ndende za chitedzo chokhwim, dende za chitedzo chapakati, ndi ndende za chitedzo chochepa
3. Ingakhale muselo ndi mu ndende ndi malo a anthu olakwa, koma iwo ndi osiyana. Akayidi aku ndende ndi omwe ayesedwa ndi kugamulidwa kuti ndi olakwa. Selo ndi komwe akayidi amafikirfa akagwidwa. Akayidi ambiri omwe amakhala mu selo amakhala kuti sanapezedwe olakwa ndi mulandu wina uliwonse. Ambiri amakhala kuti akusungidwa kutikirira

kukayesedwa. Ena amakhala kuti akudikirira chigamulo. Ena amakhala kuti akugwira milandu yaying'ono yomwe sakuyenerakupita ku ndende.

4. Malo ena osungirako akayidi omwe akambidwa mu chapatalachi ndi:  
-Nyumba ya theka  
-Msasa wapa msewu, msasa wa moto, msasa wa munkhalango, kapena kugwira ntchito mminda  
-Ndende za ana
5. Fananizani yankho lanu ndizokambirana za mitundu ya akayidi mu chapatalachi.

### **CHAPUTALA 11**

1. Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wocokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu. (Aroma 13:1)
2. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za chapatalachi
3. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za chapatalachi
4. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za chapatalachi
5. Onetsetsani kупедза mndandanda wa malamulo akavakidze ndi chitedzo a kundende komwe mukutumikira.

### **CHAPUTALA 12**

1. ...wolangiza iwo akutsutsana mofatsa; ngati kapena Mulungu awapatse iwo citembenuziro, kukazindikira coonadi, ndipo akadzipulumutse ku msampha wa mdierekezi, m'mene anagwidwa naye, ku cifuniro cace. (2 Timoteo 2:25-26)
2. Lamulo loyamba ya kapangidwe ka ubwezi ndi akayidi ndikuphudzira ndi kutsatira malamulo.
3. Fananizani yankho lanu ndi malamulo opangira ubwezi ndi akayidi.

### **CHAPUTALA 13**

Chilibe mafunso oziyesa nokha.